

# MOYO WA PAULO

VERNA SAVAGE

# MOYO WA PAULO

Verna Savage

Losindikizidwa ndi:-

**BIBLE WAY CORRESPONDENCE SCHOOL**
**P.O. Box 292, Lilongwe, Malaŵi**

ZA M'KATIMU

MALANGIZO KWA ONSE

MAWU OYAMBA


PHUNZIRO TSAMBA

1. KUBADWA KWA PAULO........................ 1
2. PAULO KU DAMASIKO........................ 3
3. PAULO AYAMBA UTUMIKI WAKE................ 6
4. PAULO ABWERERA KWAWO..................... 9
5. PAULO AYAMBA ULENDO WAKE WACHIWIRI........12
6. PAULO KU ATENE NDI KU KORINTO.............15
7. ULENDO WACHITATU WA PAULO.................19
8. PAULO KU YERUSALEMU.......................23
9. PAULO PAMASO PA FESTO.....................26
10. PAULO KU ROMA............................30
11. PAULO M'NDENDE...........................34
12. MASIKU OTSIRIZA A PAULO..................37

# MALANGIZO KWA ONSE

Maphunziro a Bible Way Correspondence (a pa mtokoma) ndi okozedwera iwo amene sanakhale pa maphunziro a Buku Lopatulika chiyambire. Ngakhale zili choncho, maphunzirowa akhoza kuthandizanso anthu amene akhala akuphunzira Buku Lopatulika kwa nthawi yaitali. CHOLINGA cha maphunziro amenewa ndi chakuti anthu onse azindikire chikonzero cha Mulungu cha chipulumutso, ndiponso kuphunzitsa anthu kuti amvetsetse Mawu a m'Buku Lopatulika, ndi kutukula moyo wa uzimu wa mkhristu aliyense.

BUKU LOPATULIKA likhale chifupi nanu pophunzira maphunziro amenewa. Muwerenge mosamalitsa bwino ndime zonse zimene zatchulidwa zopezeka m'Buku Lopatulika. Ngati mwapeza mawu amene simukumvetsetsa kutanthauza kwake, pezani ndime yomweyo m'Buku Lopatulika m'chichewa cha makono kapena buku la matanthauzo a mawu a m'Buku Lopatulika limene lili m'chingelezi (Bible Dictionary).

KUSINTHA MALO: Ngati mwachoka kumalo kumene munali kulandirira makalata anu, chonde dziwitsani mwamsanga a Director a Bible Way.

NAMBALA YA WOPHUNZIRA: Munthu aliyense akayamba maphunziro a Bible Way, amapatsidwa nambala yakeyake. Nambala imeneyi ndi yofunika kwambiri chifukwa maphunziro a munthu aliyense amasungidwa mogwirizana ndi nambala yake. Tsono pamene mufuna kulemba kalata kwa Director wa Bible Way, onetsetsani kuti mwalemba:

DZINA LANU, NAMBALA YANU NDI ADIRESI YANU.

IYI NDIYO NAMBALA YANU..................

CHIDZIWITSO. Kuti mulandire satifiketi yanu ya Marko gawo I, muyenera kulemba mayeso anu ndi kutitumizira pasanafike pa

..............................

## MAWU OYAMBA

M'bukuli tidzakhala tikuphunzira za Paulo. Tidzaphunzira za kumene anabadwira, m'mene analili ndi kumalo kumene analalikirako.

Moyo wa Paulo unalembedwa m'Chipangano Chatsopano m'buku la Machitidwe. Muyenera kuwerenga buku lonse la Machitidwe pamene mukuphunzira bukuli.

Kuphunzira za moyo wa Paulo nkofunika kwa ife chifukwa tikhoza kutengera zitsanzo zambiri za zimene anachita pofuna kuthandiza miyoyo yathu m'masiku ano.

PHUNZIRO I

MUTU WA PHUNZIRO: KUBADWA KWA PAULO

MAWU OWERENGA: Machitidwe 21:39; 22:3; 27-28

MAWU APA MTIMA: "Ukumbukirenso Mlengi wako masiku a unyamata wako." Mlaliki 12:1

M'phunziro lino tiyamba kuphunzira za moyo wa Paulo. Dzina lake anali Saulo poyamba m'Chihebri ndipo m'Chigriki (m'Chihelene) anali Paulo. Iye anali kutchedwa Saulo mpaka pa nthawi imene anatembenuka. Paulo anali Myuda ndipo anali wokondwa kukhala wa mtundu umenewu. Iye anali wochokera ku m'badwo wa Benjamini. Paulo analinso mbadwa ya Chiroma.

## NZIKA YA KU TARINSO

Paulo anabadwa nthawi imodzi ndi Yesu Khristu. Iye anabadwira ku Tariso, mzinda wa patsogolo pa nthawi imeneyo. Tariso anali pa mtunda wa 1 Kilometre kuchokera ku nyanja ya Mediterranean; ndipo unali mzinda waukulu wa malonda. Unalinso mzinda waukulu umene unali ndi sukulu zambiri za pamwamba. Ophunzira ochokera m'sukulu zotchuka mu ufumu wonse wa chiroma, anali kupita ku Tariso kukapitiriza maphunziro awo. Munzindamu munali kukhala anthu a chigriki ndi anthu ochokera kum'mawa, kuphatikizanso ndi mitundu ina.

Mumzinda umenewu Paulo anaphunzira kakhalidwe ka anthu amitundu. Tsono pamene nthawi inafika, anali munthu wozindikira m'mene angalalikirire kwa amitundu Uthenga wabwino wa Khristu.

## MAPHUNZIRO AKE

Malinga ndi mwambo wa chiyuda, mwana aliyense wa mwamuna anali kuphunzira mokwanira. Tsono Paulo, pokhala mwana wa Myuda weniweni, anaphunzira kwambiri. Iye anaimba sukulu ya pulaimale kwawo. Kenaka, pamene anali ndi zaka 13 mpaka 15, anatumizidwa ku Yerusalemu kukapitiriza maphunziro a chilamulo cha chiyuda.

Paulo anali ndi mwawi wophunzitsidwa ndi Gamalieli, mphunzitsi wa pamwamba ndi wotchuka pa nthawiyo. Paulo anayenera kukhala kuti anali mwana wa sukulu wa nzeru kwa-

mbiri ndipo zioneka kuti ngakhale Gamalieli amene anali mphunzitsi wake, anali kumlemekeza kwambiri.

## ABWERERA KU TARISO

Pamene Paulo anatsiriza maphunziro ake ku Yerusalemu anabwerera ku mzinda wa kwawo ku Tariso. Iye anali wokonzeka kuyamba ntchito tsopano. Makolo ndi aphunzitsi ake anali kumunyadira. Ndikhulupirira kuti m'zaka zingapo zotsatira, anakhala m'Tariso monga mphunzitsi wamkulu amene anali kutchedwa Rabbi m'chihebri. Tilibe mbiri yolembedwa yonena za iye m'zaka zimenezi kufikira nthawi imene anapitanso ku Yerusalemu, Stefano atangotsala pang'ono kuphedwa. Paulo ayenera kuti anamvapo za bungwe la chikhristu limene linali kutsutsa chikhulupiriro cha chiyuda. Iye anafuna kuti apite kukateteza chikhulupiriro cha makolo ake. Iye anali ndi Ayuda anzake pamene anali kuzengedwa mlandu.
Ngakhale kuti iye sanaponye nawo mwala pakumupha Stefano, anabvomereza kuti ayenera kuphedwa. Iye anagwirizana ndi maganizo a anthu aChiyuda anzake. Anaonerera kufa kwa Stefano. Ngakhale kuti pa nthawi imeneyi sanali kuzindikira, kuphedwa kwa Stefano kunakhala mbali yofunika mkusankha kwake potsatira Yesu.

## KUZUNZA AKHRISTU

Paulo anali m'tsogoleri pakati pa Ayuda. Atsogoleri akale anatula pansi udindo wawo kuti ampatse mwawi Paulo wotsogolera pozunza akhristu. Paulo mwini wake akufotokoza zimene anali kuchita zosagwirizana ndi chikhristu. "Ndinazunza akhristu mpaka kuwapha, kuwamanga ndi kukawatula m'nyumba za ndende, ndita]andira chilolezo kwa akulu a nsembe, ndipo pamene anali kukaphedwa, ndinali m'modzi wobvomereza kuti aphedwedi. Nthawi zambiri m'masunagoge anali kuweruzidwa ndi kuwaumiriza kuti akane Ambuye wawo. Ndinawapsyera mtima kwambiri ndi kuwatulutsira kunja kwa mzinda."

Paulo anali Myuda weniweni ndipo anali kuganiza kuti akuchita bwino poononga miyoyo ya akhristu. Iyi inali nthawi yakusadziwa, asanazindikire chikondi ndi chisomo cha Ambuye ndi Mpulumutsi wathu Yesu Khrsitu.

00000o00000

PHUNZIRO 2

**MUTU WA PHUNZIRO: PAULO KU DAMASÍKO**

**MAWU OWERENGA:** Machitidwe 9:3-20

**MAWU APA MTIMA:** "Ndipo pomwepo m'masunagoge analalikira Yesu, kuti Iye ndiye Mwana wa Mulungu." Machitidwe 9.20

Kusandulika mtima kwa Paulo chinali chinthu chimodzi chachikulu chimene chinachitika m'mbiri ya dziko lapansi. Paulo pa nthawi imeneyi ndi amene anali ndi udindo wotsekera akhristu zikwizikwi m'ndende. Ndipo tsopano anali pa ulendo wopita ku Damasiko, mzinda waukulu m'dziko la Syria, kukathamangitsa akhristu kumeneko.

## PAULO PA ULENDO WA KU DAMASIKO

Pali umboni utatu wolembedwa za kusandulika mtima kwa Paulo m'Chipangano Chatsopano. Luka akutiuza zimene anali kuchita Paulo poyamba ndi zimene zinachitika pa ulendo wa ku Damasiko. Tsono Paulo mwini wake anafotokoza kwa nthawi ziwiri ndi pakamwa pake za zimene zinamuchitikira. (Umboni wonsewu ukupezeka m'buku la Machitidwe).

Paulo anali munthu woopsya kwa Akhristu onse a ku Yerusalemu. Iye anakwanitsa cholinga chake chothamangitsa Akhristu ndi kuwalamulira kuti akhale chete mumzinda wa Yerusalemu. Iye analandira uthenga kuti ku Damasiko kunali akhristu ambiri. Mzinda wa Damasiko ndi wotalikirana ndi mzinda wa Yerusalemu ndi 250 kilometres. Iye anaganiza zopitako kukapereka chizunzo kwa akhristu a kumeneko. Iye analandira zilolezo zoyenera kwa akuluakulu kuti akatenge akhristu kumeneko ndi kubwera nawo omangidwa ku Yerusalemu. Iye ndi gulu lake anawuyamba ulendo wonka ku Damasiko. Unali ulendo wautali wotenga masiku asanu ndi limodzi kapena asanu ndi awiri ndipo pamene ulendowu unali mkati m'nyamata ameneyu wa mphamvu ndi wa nzeru anali ndi nthawi yambiri yoganizira bwino. Mwina anayamba kudabwa ndi zimene anali kuchita. Sanathe kuiwala imfa ya Stefano amene anafa mwachifatse. Sanathe kuiwala pemphero la Stefano pamene anali kumponya miyala "asanagone". Paulo anafunitsitsa kuchita chinthu cholondola, koma anavutika ndi mafunso amene anali kumbwerera ndipo sanathe kuwayankha. Choncho anapitirirabe ulendo wa ku Damasiko.

## KUSANDULIKA MTIMA KWA PAULO

Mbiri inamveka kale ku Damasiko kuti Paulo anali kubwera iye asanafikeko. Kusandulika mtima kwake kunachitika atatsala pang'ono kufika mumzinda wa Damasiko. Dzuwa lili pa

mutu, kunadza kung'anima kwadzidzidzi mozungulira Paulo ndi gulu lake. Iye anagwa pansi mumdima wa ndiwe yani ndipo anamva akuti naye,

"Saulo Saulo, undilondalonderanji?"

Iye anafunsa, "Ndinu yani Ambuye?"

Yesu anayankha nati, "Ndine Yesu amene umlondalonda; komatu, uka nulowe m'mudzi, ndipo kudzanenedwa kwa iwe chimene uyenera kuchita." Paulo anadzuka nazindikira kuti sanali kutha kuona. Ena mwa anthu amene anali nawo anamgwira dzanja kulowa naye mu Damasiko. Kwa masiku atatu, Paulo anali wakhungu ndipo sanadye kapena kumwa kanthu. Zoterezi zinamsinthiratu Paulo. Tsopano Mfalisi wonyada uja anakanthidwa, anali kunjenjemera, kufufuza kuti chili kutsogolo kwanga nchiyani? Anali kukanirira kwa wina kuti amtsogolere. Iye anapita ku nyumba ya Yudasi nalowa m'chipinda chake. M'menemo anakhala masiku atatu opanda chakudya kapena madzi. Pa masiku amenewa Paulo anasala ndi kupemphera. Moyo wake wonse unasinthika kaamba ka kukumana ndi Yesu. Tsopano inafika nthawi yomanga moyo wake pa khristu.

## HANANIYA

Hananiya anali m'modzi mwa aphunzitsi pakati pa akhristu. Iye anali kukondedwa ndi kulemekezedwa ndi onse amene anamdziwa.

Hananiya anaona masomphenya ndipo anamuuza kuti apite kunyumba ya Yudasi kukafunsa za Saulo wa ku Tariso. Hananiya anachita nthumanzi chifukwa anamva za nkhaza za munthu uyu wotchedwa Saulo zimene anachitira akhristu. Mwina iye anadziwiratu kuti cholinga cha Saulo pofika ku Damasiko chinali chodzazunza akhristu amene. Koma Ambuye anamtsimikizira Hananiya kuti panalibe chifukwa chochitira mantha konse. Choncho Hananiya anapita kukamuona Paulo. Anasanjika manja ake pa mutu pa mfarisi wachinyamatayu, ndipo anamutcha, "Mbale Saulo," namuuzanso kuti amene analankhula naye pa njirayo anali Yesu. Ndipo maso a Paulo anatsekuka ndipo anapatsidwa chipatso cha Mzimu Woyera. Zitatha izi anabatizidwa kapena ndi Hananiya yemweyo.

## PAULO AYAMBA KULALIKIRA

Ndi chinthu chosadabwitsa kuti mtumwi watsopanoyu anayamba kulalikira pasanapite nthawi. Iye anayamba kulalikira, za Yesu ndi kunena poyera kuti Yesu anali Mwana wa Mulungu. Ophunzira onse anazizwa ndi kusinthika kodabwitsa kwa Paulo. Ayuda amene anamva iye akulalikira sanakhulupirire kuti anali yemwe uja. Koma Paulo anakula mumphamvu mosabwerera pa ulaliki wake.

Paulo anapita ku dziko la Arabia kumene anakakhalako

zaka zitatu. Iyi inayenera kukhala nthawi yake yophunzira ndi kusinkhasinkha pofuna kuti akonzekere ntchito yofunika imene inagona kutsogolo kwake.

Atakhala zaka zitatu ku Arabia, Paulo anabwerera ku Damasiko kumene anthu anamva Uthenga wake ndi chidwi. Koma posakhalitsa, Ayuda anafunafuna kuti amuphe. Choncho ophunzira anamzembetsa. Anamuika m'dengu lomangirira ndi zingwe namtulutsira kunja kwa khoma usiku.

Paulo anayamba kuzindikira kuzunza kumene anakuchita pa Akhristu chifukwa iyenso anali m'modzi wa iwo tsopano. Kuyambira nthawi imeneyi, Ayuda anakhala akufunafuna kuti amuphe. Iye ndi amene anali woyenerera kulalikira Uthenga Wabwino kwa Ayuda ndi amitundu omwe. Iye anakulira mumzinda wa Tariso kumene kunali kukhala amitundu ambiri ndipo anakhala naphunzira monga Myuda.

00000o00000

PHUNZIRO 3

MUTU WA PHUNZIRO: PAULO AYAMBA UTUMIKI WAKE

MAWU OWERENGA: Machitidwe 9:19-22; 11:25-26

MAWU APA MTIMA. "Ndipo ophunzira anayamba kutchedwa Akhristu ku Antiokeya." Machitidwe 11:26

M'phunziro lino tiyamba kuphunzira za kutumiza wa mishoni ku dziko lina, zimene zinayambika ndi Akhristu oyamba. Ichi sichinali chikonzero cha munthu koma cha Mulungu kuti Uthenga wabwino ufalikire ku maiko onse ndi kwa mitundu yonse ya anthu padziko lapansi. Yesu anati,

"Ndipo ngati ndikwera kuchokera m'dziko lapansi, ndidzadzitengera anthu onse kwa ine ndekha."

Iye anaphunzitsa ophunzira ake pokhudza utumiki wa ku dziko lonsewu. Kutumidwa kumene Yesu anawatumiza ophunzira ake kunali kuwatuma ku maiko onse. Kunali kobvuta kwa ophunzira aja kuyamba ntchito imeneyi ngakhale Yesu atauka ndi kukwera kumwamba. Mwina atumwiwa anali kuyembekeza kukhala m'Yerusalemu koma mazunzo anachuluka kwambiri kotero kuti anabalalitsidwa ku madera osiyanasiyana. Choncho konse kumene anathawira anakhala otumidwa kukalalikira Uthenga wabwino ngakhale kuti sanaganizire zokhala ndi dongosolo lotere. Koma Akhristu amenewa anasowa wina kuti awatsogolere, ndi kukonza zoyenera kuchita, ndi kuwatsogolera kukalalikira ku mitundu ina. Mtsogoleri ameneyu anali Paulo. Patatha zaka khumi chitembenukire, anakonzeka kutsogolera utumiki wa mpingo umenewu.

## MPINGO WA KU ANTIOKEYA

Antiokeya unali umodzi mwa mizinda yotchuka yachiroma pa nthawi imeneyo ndipo unali ndi anthu oposa 500,000.

Alaliki oyamba amene anafika ku Antiokeya kuchokera ku Yerusalemu, analinga zodzalalikira kwa Ayuda amene anali kukhala mumzindamu. Koma ena ochokera ku Cyprus ndi ku Kirene anayamba kugwira ntchito pakati pa anthu achigriki. Uku kunali kuyamba kwa kufikitsa Uthenga Wabwino kwa anthu a mitundu. Kuyambira pachiyambi pomwe mpingo unali ndi mphamvu. "Dzanja la Ambuye linali pa iwo: ndipo chiwerengero cha okhulupirira chinali kukula, nabwerera kwa Yehova."

Mpingo watsopanowu, umene anthu a mitundu yosiyanasiyana anali kupembedza, unakhala umodzi mwa mipingo ya mphamvu pa nthawiyo. Ili ndi phunziro kwa ife lero lino. Ngati titaiwala zosankhana kapena kukhala ndi maganizo oipa

pa wina ndi mnzake chifukwa chakuti ali ndi khungu losiyana ndi lako, ndi kupembedza Mulungu mumzimu ndi nchoonadi, mipingo yathu ikhoza kukhala ndi mphamvu monga m'mene unalili mpingo umenewu.

Pansi pa utsogoleri wa Baranaba, mpingo unakula kwambiri kotero kuti anasowa womthandiza. Pamene Paulo anabwera pa mpingowu kuchokera ku Tariso kudzathandiza ntchito ya mpingowu, unakulirakulirabe. Kenaka, Mpingo unayamba kukhala ndi chidwi ndi anthu a mitundu ina. Mpingo unazindikira ntchito yake yofalitsa Uthenga Wabwino kwa mitundu yonse. Mpingo wamphamvu umenewu unayenera kukhala ndi ulemu wotumikira monga likulu la kulalikira Uthenga Wabwino kwa anthu amene sali Ayuda. Kunali ku mpingo umenewu kumene atumwi anayamba kutchedwa Akhristu.

## NTCHITO YA MZIMU WOYERA

Werengani Machitidwe 13:1-2. Tikumva kuti pamene atsogoleriwa anali kupemphera ndi kusala Mzimu Woyera analankhula nawo nati, "Mundipatulire Ine Baranaba ndi Saulo ku ntchito imene ndinawaitanirako." Mawuwa akupitirira ndi kunena kuti anawaika manja nawatumiza kuti apite kukagwira ntchito imeneyi. Kusowa kwa atsogoleri awiriwa ku mpingo wa ku Antiokeya kunali kosaiwalika, komabe anachiyesa cha mwayi kukagawa Uthenga Wabwino wotere ku dziko lonse lapansi.

## ANAYAMBA ULENDO WAWO WOYAMBA

Baranaba, Paulo ndi Yohane Marko, mnyamata wochokera ku Yerusalemu, anayamba ulendo wawo. Baranaba, pokhala iye wamkulu, ndi amene anali kuyesedwa monga mtsogoleri. Paulo ndi Baranaba anali abwenzi okondana kwambiri ndipo aliyense anali kuyamikira mnzake. Yohane Marko anapita nawo monga wothandiza. Iye anali mwana wa Mariya amene anali mkhristu wokhulupirika. Yohane anali msuweni wake wa Baranaba.

Iwo anayenda pa ngalawa kupita ku Selukeya ndipo anayenda mtunda wa 100 kilometres ku Salami ku gombe cha kummawa kwa dziko la Cyprus. Ku Cyprus kunali kwawo kwakale kwa Baranaba.

Atumwiwa anachezera malo onse ofunika pa chilumba cha Cyprus nafika ku Pafo. Ku Pafo anakomana ndi anthu awiri a maudindo a pamwamba. Msing'anga wa matsenga wotchedwa Elima Bar-Yesu ndi Sergio Paulo amene anali bwanamkubwa wa pa chilumbacho. Sergio Paulo anatumiza mthenga kwa Paulo ndi Baranaba kuti abwere adzamuuze Uthenga wa Mulungu. Tsono pamene atumwi anali kumuuza Sergio Paulo za Yesu, Elima anafuna kuwaletsa. Kenaka Paulo anamdzudzula nati, "Wodzala ndi chinyengo chonse ndi chenjerero lonse," Ndipo anakhala

wakhungu kwa kanthawi. Sergio Paulo anakhudzidwa kwambiri nakhulupirira chiphunzitso cha Ambuye.

Kuyambira pa nthawi imeneyi Luka akuwatchula atumwiwa kuti "Paulo ndi gulu lake" kapena "Paulo ndi Barnaba."

ULENDO WOPITA KUMENE ANALINGA

Paulo ndi gulu lake ananyamuka ulendo wopita ku Perge wa ku pamfuliya. Pano Yohane Marko anawasiya atumwiwa nabwerera ku Yerusalemu.

Paulo ndi Baranaba anapita ku Antiokeya Mpisidiya. Paulo anapita ku Sunagoge ndipo anakalalikirako Uthenga wa Yesu Khristu. Uthenga wake unakhudza anthu ambiri ndipo anafuna kuti Paulo adzawalalikirenso. Tsiku la Sabata linzakeli, Paulo analalikiranso ndipo pafupifupi anthu a mumzinda wonse anadza kudzamvera Uthenga. Izi zinakwiyitsa Ayuda. Paulo anawauza kuti anapereka mwayi kwa Ayuda kuti alandire Uthenga umenewu. Tsono pakuti Ayuda anaukana, Paulo ndi Baranaba anatembenukira kwa anthu a mitundu. "Ndipo pakumva ichi a mitundu anakondwera, nalemekeza mawu a Mulungu; ndipo anakhulupirira onse amene anaikidwatu ku moyo wosatha. Ndipo mawu a Ambuye anabukitsidwa m'dziko lonse." Uthenga Wabwino unayambika m'mitima ya anthu aunyinji a mitundu.

Ayuda anaukira Paulo ndi Baranaba nawatulutsira kunja kwa Mzinda.

Kuyenda mtunda wa 120 kilometres cha kum'mawa kwa Mzinda wa Antiokeya kunali Mzinda wotchedwa Ikoniyo. Paulo ndi Baranaba anapita ku Sunagoge kumene Paulo analalikira. Ambiri analandira Yesu Khristu kukhala Mpulumutsi wawo. Komanso kunali anthu otsutsana nawo kumene. Atumwiwa anachita zozizwitsa ndi zizindikiro zambiri ndipo anakhala kumeneko kanthawi nalalikira Uthenga Wabwino. Potsiriza pake adani awo aja anapanga upo ndi kuopsyeza kuti atumwiwa aphedwe. Choncho, Paulo ndi Baranaba anachoka.

00000o00000

PHUNZIRO 4

MUTU WA PHUNZIRO: PAULO ABWERERA KWAWO

MAWU OWERENGA: Machitidwe 15:1-35

MAWU APA MTIMA: "Koma tikhulupirira tidzapulumuka mwa chisomo cha Ambuye Yesu Khristu, monga iwo omwe." Machitidwe 15:11

Paulo ndi Baranaba anatulutsidwa ku mzinda wa Ikoniyo. Malo ena amene Paulo anaimako ndi ku Lustra. Mumzinda umenewu muyenera kuti munali mabanja ena a chiyuda amene anali kukhala momwemu. Pano tikudziwa za banja limodzi la chiyuda limene linalipo. Munali mayi wa masiye dzina lake Yunisi. Iye anali ndi mwana wa mwamuna dzina lake Timoteo. Mwamuna wake wa Yunisi sanali Myuda choncho Timoteo sanachite nawo mwambo wa m'dulidwe. (m'dulidwe unali wofunikira kwambiri kwa munthu kuti ayambe chipembedzo cha Chiyuda). Gogo Loisi amayi a Yunisi, anali kukhala kunyumba komweko. Paulo ndi Baranaba anawalalikira za Yesu ndipo analandira Yesu kukhala Mpulumutsi wawo.

PAULO KU LUSTRA

Pamene Paulo anali kulalikira ku Lustra, m'modzi wa anthu amene anamva Uthenga anali wolumala miyendo chibadwire ndipo sanali kuyenda. Iye anali kukhala m'mbali mwa misewu. Ayenera kuti anali munthu wopemphapempha wodziwika bwino ndi anthu onse m'deralo. Paulo anaona kuti munthu ameneyu anali ndi chikhulupiriro chofuna kuchiritsidwa. Choncho Paulo anapfuula nati, "Imirira pa mapazi ako." Nthawi yomweyo anadzuka naimirira ndi kuyamba kuyenda. Pamene anthu a mitundu anaona izi anaganiza Paulo ndi Baranaba anali milungu imene inatsika kumwamba kudzafanana ndi anthu. choncho anawatcha maina a milungu iwiri ya chigriki. Baranaba anamutcha Zewu ndipo Paulo anamutcha Herme. Anthu anayamba kukonza phwando kuti alandire ulemu wa padera. Mwamsanga Paulo ndi Baranaba anawauza bwino kuti iwo sanali milungu koma anthu anzawo. Iwo anawafotokozera cholinga cha kubwera kwawo kuti chinali chodzalalikira mawu a Mulungu. (Machitidwe 14:15-17). Choncho anthu achiyuda anapanga upo namponya Paulo miyala ndipo anangomusiya chifukwa anali kuyesa kuti wafa. Pambuyo pake abwenzi ake anampeza Paulo akali ndi moyo ndipo anamthandiza pomtulutsira ku dera lina. Kenaka atumwiwa anapita ku Derbe.

Nthawi yotsiriza ulendo woyamba inafika. Choncho anayamba kubwerera kwawo. Pa ulendo wawo wobwerera anaimanso ku Lustra, ku Ikoniyo, Antiokeya ndi Perga. Iwo anali kufuna kuwathandiza ntchito ndi kuti agwirizane bwino pokhazikizi-

kitsa mpingo. Anawathandizanso kusankha aphunzitsi oyenera ku mipingo imeneyi. Anakhazikitsa mpingo mumzinda uliwonse ndi kusankha mtsogoleri monga mbusa kapena mphunzitsi. Choncho mpingo wa anthu amene sanali Ayuda unakhazikika pa mchombo wa dziko la Asia.

## PAULO MONGA MTUMWI

Tatsata bwinobwino ulendo woyamba wa Paulo. Takhala ndi mwayi wakuona Paulo akugwira ntchito pa utumwi umene unaikizidwa mwa iye. Ntchito ya Paulo ndi Baranaba inali m'magawo anayi.

1. ANALI ALALIKI A UTHENGA WABWINO

Iwo analalikira uthenga wa Mulungu kwa namtindi wa anthu. Mauthenga amenewa anali amphamvu kotero kuti anthu ambiri analandira Yesu monga Mpulumutsi wawo.

2. ANALI APHUNZITSI

Mafunso ambiri sakanayankhidwa pamene anali kulalikira kwa anthu ambiri. Paulo ndi Baranaba anali otanganidwa kuphunzitsa ndi kupereka malangizo oyenera kwa anthu amene anadzipereka usiku ndi usana.

3. ANALI ALANGIZI

Ndi chachidziwikire kuti ntchito ya atumwiwa inali yofunika ulangizi wamphamvu. Iwo anatumikira monga abusa kwa anthu amene anasowa utumiki umenewu.

4. ANAYENERA KUKHALANSO A MAGANIZO ABWINO

Iwo anayenera kukhala ndi masomphenya a kayambidwe ka mpingo. Paulo anali munthu amene sanayambe wachita zimenezi koma dongosolo limene analikonza linakhala ndi zotsatira zopambana chifukwa timazigwiritsabe ntchito mpaka pano. Mulungu anamdalitsadi Paulo pa ulendo wake woyamba. Zochitika zopambana zazikulu zikuyembekezekanso pa maulendo ake otsatira.

## BVUTO LA MUMPINGO

Pamene atumwi aja anali kupuma ndi kukhala ndi chiyanjano ku Antiokeya, analandira mawu amene anali obvuta kwambiri komanso oopsyeza umoyo wa mpingo umene. Pfunso linali lakuti: Kodi munthu amene sanali Myuda akhoza kukhala mkhristu? Tidziwa kuti Filipo ndi Petro anakagwira ntchito pakati pa a Samaria ndipo ena anatembenuka mtima. Petro anachita umboni kuti ngakhale a mitundu akhoza kulandira

Yesu ndi kupulumutsidwa pamene Korneliyo ndi Agriki ena anapulumutsidwa ku Kaisarea. Mpingo unabvomereza Akhristu achigriki ku mpingo wa ku Antiokeya m'dziko la Syria. Koma pamene Paulo ndi Baranaba anali pa ulendo wawo, anthu anayamba kudzifunsa kuti kodi ndi kobvomerezeka kwa anthu a mitundu kukhala Akhristu? Anthu ena ochokera ku mpingo wa ku Yerusalemu anapita ku Antiokeya kukawadzidzimutsa ndi pfunso ngati limeneli. Anthu amenewa anali Afarisi ndipo anadimbikira zakuti munthu wa mwa amitundu sangakhale mkhristu chifukwa ndi wosadulidwa. Malingana ndi maganizo awo, kunali koyenera kuti munthu ayambe wakhala Myuda poyamba. Choncho kunali bvuto lalikulu ku mpingo wa ku Antiokeya chifukwa cha zimenezi.

Paulo atamva izi, anaona kukula kwa bvuto limeneli kuti kunali kwakukulu. Bvuto limeneli likanamwaza mipingo ndi kukhala yogawanikana ndiponso kuimitsiratu ntchito ya chikhristu. Choncho, Paulo anafuna kuyankha mopanda kunyengerera pa pfunso limeneli. Iye anati kudulidwa sindiko kumampulumutsa munthu ayi.

Tsono anaganiza zokatula bvutoli ku Yerusalemu, osati kuti akauzidwe zoyenera kuchita chifukwa mpingowu unalibe likulu lolandirira malamulo, koma chinali chifukwa chakuti anthu a ku Yerusalemu ndi amene anayamba kufunsa pfunso limeneli. Paulo anafuna kuonetsa kuti ngakhale Akhristu a ku Yerusalemu ayenera kugwirizana naye pa nkhani imeneyi kuti mipingo ikhale yomasuka.

Ku Yerusalemu atsogoleri a mpingo anaitanidwa ku msonkhano wa padera. Pa msonkhanowu, Petro anachitira umboni za kukumana kwake ndi Korneliyo wa mwa amitundu. Paulo ndi Baranaba anachitira umboni za madalitso amene analandira pochitira umboni kwa anthu amitundu. Pfundo yotsiriza inali chigonjetso chachikulu ku mbali ya Paulo. Pfundo yake inali yakuti alembe makalata ku mipingo yonse kuwadziwitsa anthu kuti m'dulidwe ndi miyambo ya Chiyuda sindiyo yomuyenereza munthu amene sali Myuda kukhala Mkhristu.

Mpingo wa ku Yerusalemu unasankha Yuda ndi Sila kuti abwerere ku Antiokeya pamodzi ndi Paulo ndi Baranaba. Pamene anafika mpingo wonse unaitanidwa kudzamva zolembedwa m'kalata muja. Ataiwerenga, onse anadzala ndi chimwemwe.

Paulo ndi Baranaba anakhalabe ku Antiokeya kwa kanthawi akupuma, ndipo anaphunzitsa nalakira Mawu a Mulungu komweko.

00000o00000

PHUNZIRO 5

MUTU WA PHUNZIRO: PAULO AYAMBA ULENDO WAKE WACHIWIRI

MAWU OWERENGA: Machitidwe 16:1-40; 17:1-14

MAWU APA MTIMA: "Ndikhoza zonse mwa Iye wondipatsa mphamvuyo". Afilipi 4:13

Paulo atapuma ndi kuphunzira mumpingo wa ku Antiokeya, maganizo ake anatembenukira ku ntchito yawo imene anaichita mwa amitundu. Choncho anamfusa mnzake Baranaba kuti apitenso ku ulendo wokalalikira kachiwiri ku malo amene anakalalikira kale ndi kukawaona m'mene alili.

Baranaba anafuna kupitanso ndi Yohane Marko uja anawasiya ku Pamfuliya nabwerera ku Yerusalemu. Koma Paulo sanagwirizane ndi zimenezo chifukwa kuti anali mwana ndipo sanathe kupirira pa ulendo woyamba. Choncho awiriwa anapatukana wina kupita kwina winanso kwina. Tikumva kuti Baranaba ndi Yonane Marko anayenda panyanja kuolokera ku Cyprus. Paulo anasankha Sila nayamba ulendo wake wa chiwiri.

KUCHEZERA MIPINGO

Paulo ndi Sila anafika ku Derbe poyamba. Ndipo anapitirira mpaka ku Lustra kumene anakapeza Timoteo. Timoteo, Mkhristu watsopano, anapititsa patsogolo chikhulupiriro chake cha mwa Khristu Yesu naonetsa mphatso za utsogoleri weniweni. Timoteo anali ndi bambo wochokera mwa amitundu koma mayi wake anali Myuda choncho sanadulidwe pa mwambo wa Chiyuda. Paulo anakonza kuti Timoteo apite naye ku ulendo wake wa chiwiri. Tsono pofuna kutsutsa Ayuda ndi kunyogodola kumene anali nako pa anthu osadulidwa, Paulo anamuuza Timoteo kuti adulidwe. Sitidziwa zambiri zimene zinachitika ku Lustra koposa izi.: "Kotero Mipingoyo inalimbikitsidwa m'chikhulupiriro, nachuluka m'chiwerengero chawo tsiku ndi tsiku." Machitidwe 16:5

Pamene Paulo anakachezera mpingo wa ku Antiokeya m'Pisidiya, adaganizira zopita ku malo ena a dziko la Asia. Koma Mzimu Woyera sanawalole kupitako. Choncho anapita cha kumpoto ku Frugiya ndi ku Galatiya kumene Iye ndi anzake anayambitsa mipingo. Kenaka Paulo anakonzekera zopita ku chigawo cha Bisiniya, ndipo Mzimu sanawalolenso. Choncho anayang'ana cha kumadzulo. Kenaka Paulo, Sila ndi Timoteo anatulukira ku gombe la nyanja lotchedwa Trowa.

Usiku wina wake ku Trowa komweko, Paulo anaona masomphenya. Munthu wochokera ku Makedoniya anaimirira namuitana kuti apite ku dzikolo kukawathandiza ntchito. Maso-

mphenya amenewa anali achitsimikizo chachikulu, kotero kuti Paulo anaona kuti Ambuye ndi amene anali kufuna kuti apiteko. Choncho anakozekera zooloka nyanja kunka ku Ulaya. Nchachidziwikire kuti Luka anatsagana nawo kuyambira pamalo amenewa a ku Trowa.

## KU FILIPI

Paulo ndi gulu lake anaolokera ku Neapoli nayenda mtunda wa 15 kilometres kukafika ku Filipi. Tsiku lasabata, Paulo anapita kufupi ndi mtsinje kumene kunali malo opempherera Ayuda. Kumeneko anapeza gulu la amayi nalalikira kwa iwo Uthenga Wabwino. M'modzi wa amayiwa anali wa luso lokongoletsa nsalu ndi kuzigulitsa. Dzina lake anali Lidiya. Iye atamva Uthenga Wabwino kuchokera kwa atumwi amenewa, analandira zonse anazimva ndipo anakhala mkhristu. Iye anaonetsa chikhulupiriro chake poyera pamene anabatizidwa natsogoleranso a pa banja lake kuti akhulupirire Yesu ndi kubatizidwa. Anapempha atumwiwa kuti akhale alendo ake kunyumba kwake pa nthawi ya kucheza kwawo mumzinda umenewu. Choncho mpingo wa ku Afilipi unakhazikitsidwa ndipo amene anayamba kutembenuka ku Ulaya anali munthu wa mkazi.

Msungwana wina amene anali wodzazidwa ndi mzimu wonyasa ndipo anali kubwebweta ndi kunena za m'tsogolo, anatsatira kumene Paulo ankapita tsiku ndi tsiku. Anapanga ndalama zambiri za Mbuye wake zimene anthu anali kupereka pamene anali kuwauza za mwayi wawo wa mtsogolo. (Werengani Machitidwe 16:16-24). Paulo anamchiritsa m'Dzina la Yesu ndipo anakhala mkhristu. Iye atachiritsidwa, anakhala bwinobwino ndipo sanathenso kunena za mtsogolo monga kale. Chifukwa cha ichi Ambuye ake anapsya mtima. Anagwira Paulo ndi Sila nawatengera ku bwalo la oweruza. Iwo anakwapulidwa ndi zikoti natsekeredwa m'ndende.

## M'DINDO WA NDENDE

Wosunga akaidi (mdindo wa ndende) anatsekera Paulo ndi Sila m'ndende namangirira miyendo yawo ku matabwa.

Pakati pa usiku iwo anali kupemphera ndi kuimba nyimbo zotamanda Mulungu ndipo akaidi ena anali kungomvera. Mwadzidzidzi kunali chibvomerezi chachikulu kotero kuti maziko a nyumba ya ndendeyo anagwedezeka. Zitseko zonse zinatsekuka ndipo maunyolo a munthu aliyense anaduka. Pamene wosunga akaidiyu anadzuka naona kuti zitseko zonse zinali zotsekuka, anasolola lupanga m'chimake ndipo analalira kuchotsa moyo wake chifukwa choganiza kuti akaidi onse athawa. Paulo, mofulumira, anati, "Usadzipweteke wekha tonse tili muno."

Mdindoyo anaitanitsa nyali nalowa mkati monjenjemera, anagwa pa mapazi a Paulo ndi Sila. Anawatengera panja nati, "Ambuye ndichitenji kuti ndipulumuke?" Iwo namuyankha nati, "Ukhulupirire Ambuye Yesu ndipo udzapulumuka iwe ndi a pabanja ako."

Kenaka anamuuza Iye pamodzi ndi a pabanja lake Uthenga wa Mulungu. Pakati pa usikuwo, m'dindoyo anatengera Paulo ndi Sila padera nawatsuka mabala awo. Kenaka, mdindoyo pamodzi ndi banja lake anabatizidwa nthawi yomweyo. Patapita nthawi, anawatengera kunyumba kwake nakawapatsa chakudya. Mdindoyo ndi banja lake anasangalala kuti tsopano apeza chikhulupiriro mwa Mulungu.

Oweruza milandu aja anazindikira mochedwa kuti Paulo ndi Sila anali mbadwa za chiroma. Atadziwa ichi, anabvutika mumtima pakuti anakwapula mbadwa zimenezi pa gulu osawazenga mlandu. Oweruzawa anapita okha kwa Paulo ndi Sila kukawapepesa. Iwo anatuluka nawo panja nawapempha kuti achoke mumzinda muja. Koma Paulo ndi Sila anapita kunyumba kwa Lidiya kukaona Akhristu ndi kukawalimbikitsa kupitiriza ntchito ku Filipi.

## KU TESALONIKA

Kuchokera kwa Afilipi, Paulo ndi Sila anapita ku Tesalonika. Kwa masabata atatu Paulo analalikira m'sunagoge ndipo anapambana popindulira Yesu anthu achiyuda ndi achigriki omwe. Komanso Ayuda anachita nsanje nayamba kuchita chipolowe. Komabe ngakhale zinthu zinali choncho, asanachoke mumzinda umenewu, atumwiwa nkuti atakhazikitsa mpingo wamphamvu.

Atachoka ku Tesalonika, anapita ku Bereya. Anthu a ku Bereya anamva zimene atumwi ankanena ndipo anadzisanthulira malemba kuti aone okha ngati zimene anali kunena atumwiwa zinali zoona. Ayuda ndi Agriki ambiri anakhulupirira Uthenga Wabwino. Anthu a ku Tesalonika, makamaka Ayuda, atamva kuti anthu ambiri anatembenuka mtima ndi kukhala Akhristu, anabwera ku Bereya komweko kudzathamangitsa Paulo ndi Sila. Paulo anachokadi koma Sila ndi Timoteo amene anampeza komweko anatsala. Abwenzi ena anamtenga Paulo kuoloka nyanja kupita ku mzinda wa dziko la Greece wotchedwa Athens (Atene). Pamene abwenziwa anali kubwerera ku Bereya, Paulo anatumiza uthenga kwa Sila ndi Timoteo kuti abwere mwamsanga ku Atene.

00000o00000

PHUNZIRO 6

MUTU WA PHUNZIRO: PAULO KU ATENE NDI KU KORINTO

MAWU OWERENGA: Machitidwe 17:15-34; 18:1-17

MAWU APA MTIMA: "Koma kulani m'chisomo ndi chizindikiritso cha Ambuye Wathu ndi Mpulumutsi Yesu Khristu." 2 Petro 3:18

Mzinda wa Athens unali wokongola kwambiri. Unali mzinda wa mbiri yakale, luso losiyanasiyana, chikhalidwe cha anthu ndi kufufuza za chilengedwe. Pamene Paulo anali kuyenda mumzindamo, anaona kuti unali wodzala ndi nyumba zopembedzera, maguwa ndi magome a chipembedzo ndi zithunzi zosema ndi zoumba. Mtima wake unawawa poona zoterezi. Kenaka anaona guwa limene m'musi mwake munalembedwa kuti, "KWA MULUNGU WOSADZIWIKA." Ataona ichi, anazindikira kuti anthu a mumzinda umenewu anali kufufuza Mulungu woona. Ngakhale kuti Paulo analibe maganizo olalikira kumeneku, tsopano anaona kuti sangathe kukhalabe chete. Ayenera kulalikira poyera choonadi cha Ambuye amene ali Mpulumutsi.

PAULO ANALANKHULA KWA ANTHU

Paulo anayamba kulalikira m'masunagoge ndi m'misika. Pamene anali kulalikira, anthu anayamba kumvera ulalikiwo. Kenaka anamtengera kwa akuluakulu a mzinda. Iye anayamba kuwauza kuti Mulungu amene akumtumikira ndiye Mlengi wa kumwamba ndi dziko lapansi ndi kuti moyo wonse ndi mphamvu zichokera kwa Iye. Iye anapitirira ndi kuwauza kuti nkofunika kwa munthu aliyense kuti alape machimo ake ndi kukhulupirira Yesu amene anauka kwa akufa. Tsono pamene anangoyamba kulalikira za kuuka kwa akufa, anthu ena anayamba kuseka ndi kumunyogodola. Koma ena anati, "Tikufuna kudzamva zina za zimene mwalankhulazi." Alipo ena amene anakhulupirira.

KU KORINTO

Atachoka ku Atene, Paulo anapita ku Korinto, Korinto unali mzinda wa chuma chochuluka ndiponso wotetezedwa kwambiri. Komanso unali mzinda umene unadzala ndi uchimo wa mitundumitundu. Ayuda ambiri amene anachotsedwa ku Roma ndi mfumu ya Chiroma anali kukhala mumzindamu. M'modzi wa amenewa anali Akula ndi mkazi wake Prisila. Iwo anali omanga mahema. Anayamba kuchita bizinezi yotere ali ku Korinto komweko. Tsono Paulo atafika anaona kuti nkwabwino kuti ayambe kugwira ntchito imene anali nayo luso kuti athandizike popeza ndalama zogulira zakudya ndi zina. Ntchito imene anayamba inali yopanga mahema omwewo. Apa ndi

pamene iye anapeza mpata wokumana ndi Akula ndi Prisila. Iye anakhala nawo kunyumba kwawo ndipo tsiku la Sabata lililonse anali kupita ku nyumba yopembedza kukalalikira kwa Ayuda ndi Agriki. Iye anali kuchitira umboni za Yesu kwa anthu a ku Korinto kawirikawiri. Anapeza thandizo la ndalama kuchokera ku ntchito imene anaigwira mokhulupirika ndipo analalikira ndi kuphunzitsa konse kumene anali ndi mwawi wotero.

Paulo anakondwa kwambiri pamene Sila ndi Timoteo anafika kuchokera ku Makedoniya. Iwo anamuuza kuti mpingo wa ku Tesalonika unali wamphamvu m'chikhulupiriro cha mwa Ambuye. Ichi chinampatsa Paulo chimwemwe chosefukira pa ntchito yake ku Korinto.

ALI KOMWEKO KU KORINTO

Ntchito ya Paulo ku Korinto inakula ndi mphamvu kwambiri kotero kuti Ayuda anayamba kuchita nayenso kaduka. Bvuto limene anayambitsa linali lalikulu kwambiri kotero kuti Paulo anawauza kuti, "Mwazi wanu ukhale pa mitu yanu; ine ndilibe kanthu; kuyambira tsopano ndinka kwa amitundu."

Iye anapita ku nyumba kwa Tito Yusito amene anali kukhala pafupi ndi nyumba yopembedzeramo Ayuda. Mkulu woyang'anira nyumba yopembedzeramoyi amene dzina lake anali Krispo anakhulupirira Ambuye nakhala mkhristu iye pamodzi ndi a pabanja lake. Ambiri anakhulupirira ndipo anabatizidwa.

Usiku wa tsiku lina Paulo anaona masomphenya ndipo Ambuye anamutsimikizira kuti asaope kanthu; choncho iye anakhalako chaka chathunthu ndi theka ali konko, "naphunzitsa mawu a Mulungu mwa iwo."

Tsono pamene Galiyo anakhala bwana mkubwa, Ayuda anafuna kumchotsa ku Korinto. Iwo anamtengera Paulo ku bwalo la woweruza watsopanoyu. Kumeneko Ayuda anamnenera zakuti akuphunzitsa zinthu zotsutsana ndi malamulo a chiyuda. Koma Galiyo anawauza kuti alibe nazo ntchito zinthu zokhudza chipembedzo chilichonse ndipo anangowatulutsa.

Paulo nkuti tsopano atakhala ku Korinto kwa zaka ziwiri. Pa nthawi yaitali chonchi, iye anatha kuchita zinthu zambiri mumzinda woipitsitsawu. Ndipo tsopano inakwana nthawi yobwerera kwawo. Iye anazindikira kuti ayenera kuthandiza mipingo kukhala yokhazikika ndi ya mphamvu. Choncho pa nthawi imeneyi analemba kalata yake yoyamba ku mpingo wa ku Tesalonika.

MAKALATA A PAULO

Paulo anagwira ntchito yaikulu kupyolera m'makalata ake. Makalata amenewa sanali ofunika kwa mipingo yokhayo komanso ndi ofunika kwambiri popereka chitsanzo chabwino ku mipingo yathu masiku ano.

MAKALATA A PAULO ANALI AWA:

1. Atesalonika woyamba ndi wachiwiri. Awa analembedwa pa zaka za 52 - 53 A.D. (Ambuye atabadwa). Makalata awa amaphunzitsa za kubweranso kwa chiwiri kwa Yesu Khristu.

2. Akorinto woyamba ndi wachiwiri, Agalatiya ndi Aroma amene analembedwa mzaka 55 - 58 A.D. Makalata awa atiphunzitsa za kuti timalandira chipulumutso mwa chikhulupiriro cha mwa Khristu.

3. Afilipi, Filimomi, Akolose ndi Aefeso analembedwa mzaka za 60 - 63 A.D. Awa amaphunzitsa za umunthu ndi umulungu wa Yesu Khristu.

4. Timoteo woyamba, Tito ndi Timoteo wachiwiri analembedwa m'zaka za 65 - 67 A.D. Awa anaphunzitsa mipingo m'mene ingachitire ndi mabvuto a m'mipingo ndi abusa.

Kupyolera mkuwerenga kwa makalata amenewa, timaona mabvuto amene anakumana nawo akhristu oyamba m'mipingo mwawo. Mabvuto amenewa anali otere:

1. Analibe matchalitchi. Poyamba akhristu analibe nyumba zopempherera mo mpaka panapita zaka zopitirira zana limodzi. Iwo anali kukumana m'nyumba zawo. Mwina amatha kukumana m'mapanga, kapena pabwalo kapena m'nyumba zazikulu zimene anayenera kulipira akatha kukumana.

2. Tsiku loyamba la Sabata limene anali kukumana silinali lopuma lobvomerezeka ndi onse. Choncho iwo pa tsikuli anali kugwira ntchito. Nthawi ya mapemphero inali m'mamawa kapena madzulo akaweruka ntchito zawo.

3. Analibe zowathandiza popembedza monga masiku ano. Analibe nabuku opatulika kunyumba kwa aliyense. Analibe mabuku a nyimbo kapena matraki monga masiku ano.

4. Analibe atsogoleri ophunzitsidwa bwino. Choncho anali kudalira pa aphunzitsi amene sanaphunzitsidwe mokwanira kupatula pa nthawi yokhayo imene Paulo, Sila ndi Timoteo ndi ena anali nawo pamodzi.

Paulo nkuti atachoka ku Antiokeya zaka zitatu zapitazo,

choncho anafunitsitsa kubwererako. Paulo anachoka ku Korinto ndi Akula ndi mkazi wake. Anaima ku Efeso kumene analalikirako Uthenga Wabwino wa Khristu. Anapitirira mpaka ku Yerusalemu kumene anakhalako pang'ono kenaka anafika ku Antiokeya. Ndipo kachiwirinso anachitira umboni za njira yodabwitsa imene Mulungu anawagwiritsira ntchito ndi kudalitsa ntchito ya kwa amitundu m'dera la kumadzulo.

00000o00000

MOYO WA PAULO

KABUKU KA MAYESO

MALANGIZO KWA MUNTHU WOLEMBA MAYESO AWA

CHOYAMBA. Lembani dzina lanu, adiresi yanu ndi nambala yanu mooneka bwino m'malo amene mwapatsidwa. Onetsetsani kuti musasinthe dzina lanu kapena kalembedwe kake kuti kasasiyane ndi m'mene munalilembera poyamba maphunzirowa.

CHACHIWIRI. Yankho la pfunso lililonse lidzapezeka m'phunziro limene mwapatsidwa kapena m'ndime za m'Buku Lopatulika zimene zatchulidwa. Mukhoza kufufuza mayankho a mafunsowa poyang'ana m'phunziro limene muli kuyankha pfunso lake.

CHACHITATU. Pali yankho limodzi lokha lolondola pa pfunso lililonse. Mayankho ambiri ndi a LIWU LIMODZI lokha. Mafunso ena akhoza kuyankhidwa ndi mawu angapo ngati dzina lonse la munthu kapena udindo wake wafunsidwa kuti utchulidwe. Lembani bwinobwino yankho lake munzere umene uli pambali pa pfunso lililonse. Malo amene mwapatsidwa ndi okwanira kuyankha mafunso onse. Simuyenera kulemba mawu ambiri poyankha mafunsowa koma liwu limodzi kapena awiri ngati mwafunsidwa kutero. Mafunso akhoza kufunsidwa m'njira zosiyanasiyana: (1) pali mafunso oyankhidwa polemba liwu limodzi; (2) Liwu limodzi limene lasiyidwa pa ndime ina m'Buku Lopatulika, komabe muyenera kulemba liwu losiyidwalo pambali pa pfunso munzere monga mwakhala mukuchitira ndi mafunso ena onse. Musalembe yankho mkati mwa pfunso; (3) Mafunso ena ayenera kungoyankhidwa polemba "Inde" kapena "Iyayi"

Werengani chitsanzo chili m'munsichi kuti mumvetsetse bwino zimene muyenera kuchita.

MWACHITSANZO

<u>Genesis</u> 1. Buku loyamba M'buku Lopatulika ndi liti? Tikudziwa kuti yankho lake ndi GENESIS. Choncho lembani kuti GENESIS munzere umene uli pambali pa pfunsolo.

CHITSANZO

<u>Genesis</u> 2. Dzina la buku loyamba m'Buku Lopatulika ndi ____________________.



Chotsani Gawo Limeneli la Mayeso

Tikudziwa kuti liwu limene lasiyidwa ndi GENESIS. Choncho lembani kuti GENESIS pambali pa pfunsolo osati pa nzere uli patsogolo pa pfunsoli.

CHITSANZO

Iyayi 3. Kodi dzina la buku loyamba m'Buku Lopatulika ndi Eksodo?

CHACHINAYI: Pamene muli kulemba mayeso amenewa, werengani mosamalitsa pfunso lililonse, ganizirani bwinobwino, khalani ndi nthawi pang'ono kuti muyankhe mosalakwa. Musangolota pofuna kuyankha. Onani kuti mwawerenga ndi kufufuza m'phunziro lanu ngati yankho limene mwalemba ndi lolondola.

CHACHISANU: MUYENERA KUKHALA MUTACHITA IZI MAYESO ANU ASANACHONGEDWE:

(a) Muyenera kukhala mutawerenga ndime zonse zolembedwa m'phunziro limene mukuyankha mafunso ake.

(b) Muyenera kukhala mutaloweza ndime ya pamtima ndi kuinena kwa bwenzi lanu.

Izi zidzakuthandizani kuyankha pfunso loyamba ndi lachiwiri molondola ndi m'choonadi.

CHACHISANU NDI CHIMODZI - Onetsetsani kuti mukuyankha mafunso a maphunziro atatu onse, muwaike mu enivolopu ndi kuwatumiza kuno ku Bible Way pa positi.

CHACHISANU NDI CHIWIRI - Onetsetsani kuti mwamata sitapa yokwanira pa enivolopu. Sitidzaombola makalata amene sanamatidwe sitampa yokwanira.

Sitipereka satifiketi pakutha pa phunziro la buku lililonse m'chigawo ichi. Mukatsiriza mabuku ATATU onse ndi kuyankha bwino, mudzalandira DIPLOMA ya pamwamba. Diploma imeneyi ndi yotsimikizira kuti mwatsiriza ndi kupambana maphunziro amenewa koma sikuti ndi yofunsira ntchito ku mabungwe a Chikhristu.

## MOYO WA PAULO

DZINA ______________________ NAMBALA YA WOPHUNZIRA ________

ADIRESI YANU ______________________________________________

___________________________________________________________

### MAYESO A PHUNZIRO I

______________ 1. Kodi mwaloweza ndime ya pamtima ya pa Mlaliki 12:1, ndi kuinena kwa bwenzi lanu?

______________ 2. Kodi mwawerenga ndime za m'Buku Lopatulika zimene zatchulidwa m'phunziro I?

______________ 3. Paulo asanatembenuke mtima anali kutchedwa yani?

______________ 4. Paulo anali munthu wochokera ku mtundu uti?

______________ 5. Kodi Paulo anali mbadwa ya Chiroma?

______________ 6. Paulo anabadwira mumzinda uti?

______________ 7. M'phunzitsi wa Paulo ku sukulu ya pamwamba ya Chiyuda ku Yerusalemu anali yani?

______________ 8. Kodi ndi imfa ya yani imene Paulo sanathe kuiwala ndipo inakhudza ngakhale pa kusankha kwake kuti atsatire Yesu.

______________ 9. Kodi Paulo anakana kuti iye sanazunze Akhristu ndi kale lonse pamene anatembenuka mtima?

______________ 10. Kodi pamene Paulo anali kupha Akhristu iyeyo anali kuganiza kuti akuchita bwino?

MAYESO A PHUNZIRO 2

______________ 1. Kodi mwaloweza ndime ya pa-mtima ya pa Machitidwe 9:20 ndi kuinena kwa bwenzi lanu?

______________ 2. Kodi mwawerenga ndime za m'Buku Lopatulika zimene zatchulidwa m'phunziro 2?

______________ 3. Kodi kutembenuka mtima kwa Paulo kunalembedwa kangati m'Chipangano Chatsopano?

______________ 4. Ndi m'buku liti m'Chipangano Chatsopano m'mene munalembedwa zonse za kutembenuka mtima kwa Paulo?

______________ 5. Paulo anali kupita ku mzinda uti pamene anatembenuka mtima?

______________ 6. Ndani ananena mawu awa: "Saulo, Saulo, undilondalonderanji?"

______________ 7. Paulo anakhala wosaona masiku angati?

______________ 8. Amene anatumidwa ndi Mulungu kuti akauze Paulo za Yesu anali yani?

______________ 9. Paulo anapita kuti kumene anakakhalako zaka zitatu akuphunzira ndi kupemphera?

______________ 10. Munzere uli ku manzerewu, lembani liwu limene lasiyidwa pa ndime iyi, Machitidwe 9:25: "Koma ophunzira ake anamtenga usiku, nampyoletsa pa linga, namtsitsa ndi ______________"?

DZINA ______________________ NAMBALA YA WOPHUNZIRA __________

ADIRESI YANU __________________________________________

______________________________________________________

MAYESO A PHUNZIRO 3

__________ 1. Kodi mwaloweza ndime ya pamtima pa Machitidwe 11:26, ndi kuinena kwa bwenzi lanu?

__________ 2. Kodi mwawerenga ndime za m'Buku Lopatulika zimene zatchulidwa m'phunziro 3?

__________ 3. Munzere uli kumanzerewu, lembani liwu limene lasiyidwa pa ndime iyi: "Ndipo ngati ndikwera kuchokera m'dziko lapansi, ndidzadzitengera anthu onse kwa __________ ndekha."

__________ 4. Ndi mumzinda uti umene ophunzira anayamba kutchedwa Akhristu?

__________ 5. Pa Machitidwe 13:2, Mulungu anauza mpingo kuti umpatulire anthu awiri ku ntchito ya padera. M'modzi anali Saulo. Wina ndani?

__________ 6. Mnyamata amene anali msuweni wake wa Baranaba amene anapita nawo ngati wothandiza pa ulendo woyamba wa Paulo anali yani?

__________ 7. Ndi chilumba chiti chimene Paulo ndi gulu lake anafikako pa ulendo wake woyamba?

__________ 8. Amene anali bwanamkubwa wa chilumbacho anali yani?

__________ 9. Atumwiwa anapita kumzinda uti, ku Pamfuliya, atachoka ku Pafo?

__________ 10. Pamene Ayuda anakana Uthenga wa Paulo ndi Baranaba, iwo anatembenukira kwa yani?

MAYESO A PHUNZIRO 4

_______ 1. Kodi mwaloweza ndime ya pamtima ya pa Machitidwe 15:11, ndi kuinena kwa bwenzi lanu?

_______ 2. Kodi mwawerenga ndime za m'Buku Lopatulika zimene zatchulidwa m'phunziro 4?

_______ 3. Ndi mumzinda uti umene banja la Yunisi linali kukhala?

_______ 4. Mwana wa mwamuna wa Yunisi anali yani?

_______ 5. Pamene Paulo anachiritsa munthu wopunduka, anthu anawapatsa iye ndi Baranaba maina a milungu yawo. Wina anali kutchedwa Herme, wina anali yani?

_______ 6. Paulo anakakhala zaka zingati pa ulendo wake woyamba?

_______ 7. Ndi Akhristu a ku mzinda uti amene anafunsa ngati munthu amene sanali Myuda angathe kukhala mkhristu?

_______ 8. Pamene Akhristu mumzinda anakomana pa nkhani yokhudza mdulidwe, ndani amene anagwiranso ntchito ndi amitundu kupatulapo Baranaba ndi Paulo?

_______ 9. Anthu awiri anabwerera ku Antiokeya pamodzi ndi Baranaba ndi Paulo. Mmodzi anali Yuda nanga wina anali yani?

_______ 10. Kodi atsogoleri a mpingo a ku Yerusalemu anabvomerezadi kuti mdulidwe ndi woyenerera kuti munthu apulumutsidwe?

MOYO WA PAULO

DZINA______________________NAMBALA YA WOPHUNZIRA__________

ADIRESI_________________________________________________

________________________________________________________

MAYESO A PHUNZIRO 5

____________________1. Kodi mwaloweza ndime ya pamtima ya pa Afilipi 4:13, ndi kuinena kwa bwenzi lanu?

____________________2. Kodi mwawerenga ndime za m'Buku Lopatulika zimene zatchulidwa m'phunziro 5?

____________________3. Anapita ndi Baranaba pa ulendo wake wachiwiri ndani?

____________________4. Anapita ndi Paulo pa ulendo wake wachiwiri ndani?

____________________5. Ndani anakampeza Paulo pamene anali ku Lustra?

____________________6. Ndani anakomana ndi Paulo ndi gulu lake ku Trowa?

____________________7. Ku Trowa Paulo anaona masomphenya. Munthu amene anamuona m'masomphenya anali kumuitana kuti apite ku dziko liti?

____________________8. Ndani amene anayamba kutembenuka mtima ku Ulaya?

____________________9. Pa Machitidwe 16:15 akutiuza zinthu ziwiri zimene Paulo ndi Sila anachita pakati pa usiku ali m'nde-nde. Anaimba nyimbo zotamanda Mulungu nanga anachitanso chiyani?

____________________10. Atachoka ku Filipi, atumwiwa anapita kuti?

MAYESO A PHUNZIRO 6

__________ 1. Kodi mwaloweza ndime ya pamtima ya pa 2 Petro 3:18, ndi kuinena kwa bwenzi lanu?

__________ 2. Kodi mwawerenga ndime za m'Buku Lopatulika zimene zatchulidwa mphunziro 6?

__________ 3. Kodi ndi ku mzinda uti kumene kunali guwa limene linalembedwa, "Kwa mulungu wosadziwika?"

__________ 4. Kodi Paulo anali ndi luso la mtundu wanji limene anagwira nalo ntchito ku Korinto?

__________ 5. Dzina la mkazi wa Akula anali yani?

__________ 6. Kumanzereku, lembani liwu limene lasiyidwa pa ndime iyi: "Mwazi wanu ukhale pa __________ yanu."

__________ 7. Paulo anakhala ku Korinto zaka zingati?

__________ 8. Atatu mwa makalata a Paulo analembedwa mzaka za 65 - 67 A.D. Awiri anali a kwa Timoteo nanga ina inali ya kwa yani?

__________ 9. Ndi kalata iti kupatulako za Akorinto ndi ya ku Agalatiya m'mene muli mawu akuti "Timalandira chipulumutso mwa chikhulupiriro cha mwa Khristu?"

__________ 10. Paulo anakakhala zaka zingati pa ulendo wake wachiwiri?

MOYO WA PAULO

DZINA ______________________ NAMBALA YA WOPHUNZIRA __________

ADIRESI YANU ____________________________________________

_______________________________________ ______________________

MAYESO A PHUNZIRO 7

______________ 1. Kodi mwaloweza ndime ya pamtima ya pa 2 Atesalonika 3:13, ndi kuinena kwa bwenzi lanu?

______________ 2. Kodi mwawerenga ndime za m'Buku Lopatulika zimene zatchulidwa m'phunziro 7?

______________ 3. Ndi mumzinda uti m'mene Akhristu anali kubvutika chifukwa chosowa chakudya?

______________ 4. Paulo analemba makalata angati pa ulendo wake wa chitatu?

______________ 5. Likulu la dziko la ku Asia linali kutchedwa chiyani?

______________ 6. Paulo anakhala zaka zingati ku Efeso?

______________ 7. Dzina la mulungu amene anali kumupembedza ku Efeso ndani?

______________ 8. Kalata yoyamba ya kwa Akorinto inalembedwa Paulo ali kuti?

______________ 9. Pamene Paulo anaima ku Trowa, ndi tsiku liti limene Akhristu anali kupembedza?

______________ 10. Munzere uli kumanzerewu, lembani mawu amene asiyidwa pa ndime iyi: "Kupatsa ______________________

MAYESO A PHUNZIRO 8

__________ 1. Kodi mwaloweza ndime ya pamtima ya pa Aefeso 6:10, ndi kuinena kwa bwenzi lanu?

__________ 2. Kodi mwawerenga ndime za m'Buku Lopatulika zimene zatchulidwa m'phunziro 8?

__________ 3. Paulo anakhala zaka zingati pa ulendo wake wachitatu asanabwerere ku Yerusalemu?

__________ 4. Ndani amene anali mkulu wa nsembe pa bwalo lalikulu la Chiyuda limene linali kuzenga mlandu Paulo?

__________ 5. Panali magulu awiri m'bwalo lalikulu la Chiyuda, lina linali la Afarisi nanga lina linali la ayani?

__________ 6. Ndi kumzinda uti kumene Ambuye anamutsimikizira Paulo kuti adzapita?

__________ 7. Paulo anatengedwa kupita ku mzinda uti pamene Ayuda a ku Yerusalemu anakonza chiwembu chofuna kumupha.

__________ 8. Paulo anakhala zaka zingati m'ndende asanamasulidwe?

__________ 9. Paulo analembera yani kalata yonena za kumangidwa kwake pamene anati: "Abale anga ndifuna kuti mudziwe kuti zimene zandigwera, makamaka zathandiza kufalitsa Uthenga Wabwino.

__________ 10. Munzere uli kumanzerewu lembani liwu limene lasiyidwa pa ndime iyi: "Chotsalira, tadzilimbikani mwa Ambuye, ndi __________

MOYO WA PAULO

DŻINA____________________ NAMBALA YA WOPHUNZIRA__________

ADIRESI YANU________________________________________

____________________________________________________

## MAYESO A PHUNZIRO 9

________________ 1. Kodi mwaloweza ndime ya pamtima ya pa 2 Akorinto 6:2 ndi kuinena kwa bwenzi lanu?

________________ 2. Kodi mwawerenga ndime za m'Buku Lopatulika zimene zatchulidwa m'phunziro 9?

________________ 3. Anali woweruza milandu ndani pamene Paulo anazengedwa mlandu koyambirira?

________________ 4. Anali woweruza milandu ndani pamene Ayuda anabweretsa mlandu wa Paulo kachiwiri?

________________ 5. Paulo anachita apilo kuti mulandu wake ukazengedwe kwa yani?

________________ 6. Panali pamaso pa mlendo uti pamene Paulo anafotokoza zonse zimene zinamuonekera kuyambira pa msewu wopita ku Damasiko kufikira nthawi imeneyo?

________________ 7. Mnzake wa Aristarko amene anatsagana ndi Paulo popita ku Roma anali yani?

________________ 8. Panali pafupi ndi chilumba chiti pamene ngalawa yawo inatsakamira mum'chenga?

________________ 9. Pamene Paulo anali kutolera nkhuni ndi chiyani chinamukwera pa dzanja?

________________ 10. Dzina la munthu wodziwika pa chilumbacho amene anaitanira alendo aja kunyumba kwake anali yani?

# MAYESO A PHUNZIRO 10

________________ 1. Kodi mwaloweza ndime ya pamtima ya pa Afilipi 1:21, ndi kuinena kwa bwenzi lanu?

________________ 2. Kodi mwawerenga ndime za m'Buku Lopatulika zimene zatchulidwa m'phunziro 10?

________________ 3. Kodi mzinda wotchuka wofunika kwambiri kuposa yonse unali uti pa nthawiyi?

________________ 4. Paulo anakhala m'ndende ku Roma kwa zaka zingati?

________________ 5. Paulo analemba makalata angati ali ku ndende?

________________ 6. Ndi kalata yopita kuti imene Paulo anailemba, mpingo wa kumeneko utamutumizira mitulo?

________________ 7. Amene anabwera kuchokera ku Filipi kudzatula mafuno abwino ndi kudzamthandiza Paulo anali yani?

________________ 8. Ndi kalata yopita kwa yani imene Paulo analemba kudandaulira amene anali kapolo kuti amasulidwe ndi kukhala mfulu?

________________ 9. Dzina la kapolo ameneyu anali yani?

________________ 10. Mbuye wake wa kapolo ameneyu anali kukhala kuti?

MOYO WA PAULO

DZINA ______________ NAMBALA YA WOPHUNZIRA ________

ADIRESI YANU ______________________________________

___________________________________________________

MAYESO A PHUNZIRO 11

__________ 1. Kodi mwaloweza ndime ya pamtima ya pa Aefeso 2:8, ndi kuinena kwa bwenzi lanu?

__________ 2. Kodi mwawerenga ndime za m'Buku Lopatulika zimene zatchulidwa m'phunziro 11?

__________ 3. Paulo anali kukhala mumzinda uti pamene mpingo wa kwa Akolose unayamba?

__________ 4. Ndi m'kalata iti m'mene Paulo analembamo mawu akuti, "Tsono pakuti mumdziwa Yesu mukhale monga Iye."

__________ 5. Ndi kalata iti imene Paulo analembera kwa onse?

__________ 6. Kodi Paulo anakhulupirira zakuti anthu amene sali Ayuda ndi alendo ndiponso akunja kotero kuti sangakhale ziwalo za m'banja la Mulungu?

__________ 7. Munzere uli kumanzerewu lembani liwu limene lasiyidwa pa ndime iyi, "Pakuti ife ndife __________ chake, olengedwa mwa Khristu Yesu kuchita ntchito zabwino."

__________ 8. Mogwirizana ndi buku la Aefeso, mwala wa pangodya wa kachisi amene Akhristu tonse tili kumanga ndani?

__________ 9. Lamba wa zida zathu za uzimu Paulo akuti n'chiyani?

__________ 10. Paulo ananena kuti ndani amene anamudzoza kukhala mtumwi?

## MAYESO A PHUNZIRO 12

____________________ 1. Kodi mwaloweza ndime ya pamtima ya pa 2 Timoteo 2:15, ndi kuinena kwa bwenzi lanu?

____________________ 2. Kodi mwawerenga ndime za m'Buku Lopatulika zimene zatchulidwa m'phunziro 12?

____________________ 3. Ndani amene anali mtumwi wa ku Krete?

____________________ 4. Ndani anayatsa mzinda wa ku Roma ndi kunena kuti Akhristu ndiwo anauyatsa?

____________________ 5. Paulo anamutcha mnyamata amene iye anambweretsa kwa Yesu, "Mwana wake weniweni m'chikhulupiriro." Dzina lake anali yani?

____________________ 6. Timoteo anali mbusa wa ku mpingo uti?

____________________ 7. Munzere uli kumazerewu lembani liwu limene lasiyidwa pa ndime iyi: "Pakuti ngati tidamwalira ndi Iye, tidzakhalanso moyo ndi Iye."

____________________ 8. Kodi Paulo anali kuchita manyazi chifukwa cha kukhala kwake m'ndende?

____________________ 9. Pamene Paulo analemba kalata yake yachiwiri kwa Timoteo anali ndi munthu mmodzi yekha; dzina lake anali yani?

____________________ 10. Paulo anafuna kuti Timoteo apite ndi yani kumene anali kusungidwa m'ndende?

PHUNZIRO 7

MUTU WA PHUNZIRO: ULENDO WA CHITATU WA PAULO

MAWU OWERENGA: Machitidwe 20:17-35

MAWU APA MTIMA: "Musaleme pakuchita zabwino." 2 Ates. 3:13

Paulo atangokhala nthawi pang'ono,ku Antiokeya analandira uthenga wakuti ku mpingo wa ku Galatiya unali ndi mabvuto. Choncho Paulo anayambanso ulendo wake wa chitatu umene tsopano unamtengera ku madera akutalikutali.

Kungopatulako kuti anakhala nthawi yaitali ku Efeso ndi ku Iluriko (Illyricum), ulendo wachitatu wa Paulo unali makamaka ku madera amene anapita kale ndi kugwirako ntchito.

## PAULO ANAPHUNZITSA MIPINGO

Pa maulendo awiri oyamba a Paulo, anali kupindulira anthu ambiri kwa Yesu. Koma pa ulendowu wachitatuwu, iye anaona kuti nkwabwino kuchita zinthu zina. Akhristu a ku Yerusalemu anali kuzunzika ndi njala chifukwa kunagwa njala kumeneko ndipo ambiri analibe mwawi wopezera ntchito. Choncho, Paulo anapempha mipingo ya akhristu ochokera mwa amitundu kuti apereke moolowa manja kuthandiza anzawo a ku Yerusalemu. Iye anadziwa kuti awa anali madalitso kwa opereka ndi olandira omwe. Paulo anatenga nthawi yambiri kuphunzitsa ndi kufotokoza ziphunzitso za Yesu. Akhristu achiyuda, amene amanena kuti munthu ayenera kukhala Myuda poyamba asanakhale mkhristu anafalitsa chiphunzitso chotere m'mipingo yambiri. Bvuto lalikulu linali lakuti Akhristu a mwa mitundu anakwiya ndi izi ndipo ena anayamba kubwerera m'mbuyo m'chikhulupiriro chawo. Tsono panali mipingo ina imene inali kukangana yokhayokha pa zikhulupiriro za chikhristu. Paulo anazindikira kuti nkofunika kuwaphunzitsa Akhristu a m'mipingo imeneyi kuti aime pamodzi m'chikhulupiriro cha mphamvu mwa Khristu. Pa ulendo umenewu, Paulo analemba makalata anayi kuphunzitsa anthu zikhulupiriro zoona za chikhristu.

## ZIMENE PAULO ANAPHUNZITSA

Paulo ndi woyamba komanso amene ali woposa onse pomasulira Uthenga wa Yesu Khristu. Iye ndi amene anali ndi udindo wokhazikitsa m'chitidwe wofalitsa uthenga wa chikhristu monga mwa chikhalidwe. Zotsatirazi, ndi zina zimene Paulo anaphunzitsa mipingo yakaleyo komanso zikuphunzitsabe mipingo yathu masiku ano.

1. Munthu analephera kukhala wolungama mwa iye yekha; choncho, tilephera kulandira chifundo cha Mulungu. Tonse tinalephera kukhala angwiro, palibe mmodzi wa ife amene amakhala m'moyo wangwiro.

2. Tsono pakuti munthu sangakhale wangwiro, iyeyu sangadzipulumutsenso yekha. Choncho, Mulungu anapereka njira yolandirira chipulumutso. Mulungu anapereka njira ya chipulumutsoyi chifukwa amamkonda munthu. Ichi ndi chisomo chake. Koma munthu sanachitepo kanthu kalikonse kuti apeze chipulumutso. Ichi ndi mphatso ya ulere ya Mulungu kwa anthu onse kuti onse akulandira mphatso imeneyi akalandirenso chifundo pamaso pa Mulungu. Mphatsoyi ndi ya kwa anthu onse koma ikhoza kulandiridwa mwa chikhulupiriro.

3. Yesu Khristu ndiye Momboli wa munthu aliyense. Yesu ndi amene angamchotse munthu ku nsinga za uchimo. Yense amene abvomereza chilungamo chimenechi, mwa chikhulupiriro cha mwa Khristu, amakhala mwana wa Mulungu. Koma amakhalabe ndi thupi la uchimo mwa iy· limene ayenera kuligonjetsa. Ayenera mwa chisomo cha Mulungu kugonjetsa tchimo. Chigonjetso chinalonjezedwa. Uchimo udzagonjetsedwa! Imfa kapena moyo, angelo, maufumu, zinthu za masiku ano kapena zili nkudza, mphamvu za maulamuliro, utali kapena ufupi kapena kanthu kalikonse kolengedwa, palibe mwa izi kamene kangatilekanitse ndi CHIKONDI cha Mulungu chopezeka mwa Khristu Yesu Ambuye wathu.

4. Yesu ndiye pa mchombo pa ulemerero wa chikonzero cha chipulumutso cha Mulungu. Iye ndiye Mpulumutsi wa anthu onse. Palibenso njira ina ya ku moyo wosatha yopambana Iye. Iye anadza padziko lapansi kuti adzakhale nafe ndi kufa m'malo mwathu kuti tilandire chipulumutso. Palibenso njira ina. Monganso panalibe njira ina imene inapezeka yopulumutsira munthu koposa imfa ya Yesu pamtanda kwa ifenso ndi chimodzimodzi. Yesu ndiye Mutu wa mpingo. Tsono lero Mzimu Woyera wa Yesu yemweyu akhala mwa ife kuti tikhale ndi mphamvu ya Mulungu.

KU EFESO

Paulo anakhala ku Efeso pafupifupi zaka zitatu. Efeso ndilo linali likulu la dziko la Asia. Iyi inali nthawi yaitali yokhayo imene Paulo anakhala pa malo amodzi.

Kachisi wa Artemi (mulungu wa agriki) anali wokongola kwambiri pa dziko lapansi. Kachisi ameneyu anam'manga kwa zaka 220. Anthu zikwizikwi anali kubwera kudzapembedza mulungu ameneyu wotchedwa Artemi. Izi zinampatsa Paulo mwawi wolalikira Uthenga Wabwino kwa anthu amenewa. Patapita miyezi ingapo anthu ambiri analandira Yesu kukhala

Mpulumutsi wawo ndipo anakana kupembedza Artemi.

Kwa miyezi itatu Paulo anaphunzitsa m'sunagoge. Ndipo kenaka Paulo anachita lendi ku sukulu ina kwa zaka ziwiri.

Ntchito ya Paulo ku Efeso inali yopambana kwambiri kuposa konse mu utumiki wake. Tikuuzidwa kuti onse okhala mu Asia anamva mawu a Ambuye, Ayuda ndi Ahelene omwe.

Anthu ochuluka m'chiwerengero analandira Ambuye ndipo analeka kupembedza Artemi. Chifukwa cha ichi, anthu amene anali kupembedza Artemi anayambitsa chipolowe kotero kuti Paulo anachoka poopa kutaya moyo wake.

## KUCHEZERA MAKEDONIYA

Paulo anachoka ku Efeso nabwerera ku Makedoniya kumenenso anakachezera mipingo yatsopano. Analalikira kwa kanthawi ku Trowa napitirira mpaka ku Filipi kumene Timoteo ndi Tito anatsagana naye. Mpingo wa ku Filipi unali kukhala wa mphamvu kwambiri. Inali nthawi imeneyi Paulo ali ku Filipi pamene analemba kalata yoyamba kwa Akorinto. Pasanapite nthawi yaitali analembanso kalata yachiwiri kwa Akorinto.

Anthu ambiri ku Korinto anakodwa pokhala ndi Paulo pafupi nawo. Ali mumzinda umenewu, Paulo anaphunzitsa atsogoleri a mipingo ndi kuwalangiza zoyenera kuchita pa ntchito yawo. Chifukwa china chimene Paulo anapitira ku Korinto chinali kukalimbikitsa Akhristu ndi kukapereka chopereka chokwanira ku mpingo wa ku Yerusalemu. Pamene Paulo anali ku Korinto analemba kalata kwa Agalatiya ndiponso kalata yoposa zonse ya Aroma.

Tsopano Paulo anakonzekera kubwerera ku Yerusalemu ndi ku Antiokeya. Apa ndi kuti atakakhala zaka zinayi ali muliyenda ndipo anali ndi chidwi ndi kakulidwe ka mipingo imene anaiyamba. Iye anafunitsitsa kukafika ku Yerusalemu kukapereka chopereka chimene anakhala akulandira chothandiza Akhristu a ku Yerusalemu.

Paulo anakonzera kuyenda pa sitima ya panyanja ndi anzake kunka ku Yerusalemu. Koma anamva kuti Ayuda anakonzekera kumupha akangochoka pa gombe la nyanja. chonchо Paulo anasintha maganizo. Iye ndi Luka anadzera njira yaitali ya pamtunda. Atafika ku Trowa anakumana ndi Akhristu akumeneko pa tsiku loyamba la Sabata. Apa ndi kuti atayamba kale kusonkhana pa tsikuli popembedza m'malo mwa Sabata la chiyuda. Panali pa msonkhano pamenepa, pamene Utiko, amene anakhala pa zenera uja, atagona, anagwa pansi naferatu. Abwenzi ake atapita pa malo anagwerapo anakampeza

Paulo anamdzutsa nakhalanso ndi moyo.

Tsiku linzakeli, Paulo anayenda kuchokera ku Trowa mpaka ku Aso kumene iye ndi anzake anakakwera ngalawa yopita ku Mileto. Iye analalikiranso ku Mileto.

Paulo anapitirira ulendo wake wonka ku Yerusalemu. Nthawi iliyonse imene anaima kuchezera Akhristu, iwo anali kumuchenjeza za mabvuto amene akumane nawo ngati apitirira ulendo wake. Ayuda anatsimikiza za kumupha. Koma iye anapitabe ku Yerusalemu podziwa kuti ali ndi ntchito yakuti achite. Apa anali kutsiriza ulendo wake wa chitatu wa kwa amitundu. Iye anapambana pa nkhondo yowatengera anthu a mitundu kwa Yesu, tsono anali wokonzeka kukumana ndi bvuto lina lililonse limene lingabwere.

00000o00000

PHUNZIRO 8

MUTU WA PHUNZIRO: PAULO KU YERUSALEMU

MAWU OWERENGA: Machitidwe 21:27-40

MAWU APA MTIMA: "Chotsalira, tadzilimbikani mwa Ambuye, ndi m'kulimba kwa mphamvu yake." Aefeso 6-10

Potsiriza, Paulo anafika ku Yeruśalemu atachoka kwa zaka zinayi. Akhristu anadzala ndi chimwemwe pomuona Paulo kachiwiri. Anali ndi chidwi kufuna kumva zimene Paulo anachita ndi m'mene Mzimu Woyera anakwaniritsa kupyolera mwa iye mzaka zonse anali kunjazi.

Atsogoleri onse a ku Yerusalemu anakumana ndipo anamva za m'mene anayendera Paulo. Iye anapereka ndondomeko ya zinthu zonse zimene Mulungu anachita kwa anthu amitundu kupyolera mwa iye. Atsogoleri anazizwa ndi ntchito imene Mulungu anaigwira. Iyenera kuti inali nthawi imeneyi, pamene Paulo anapereka chopereka chija ku mpingowu. Ichi chinali chopereka choperekedwa ndi Akhristu akwa mitundu kuthandiza mpingo wa ku Yerusalemu.

MABVUTO KUCHOKERA KWA AYUDA

Analipo Ayuda ambiri amene anakhulupirira ndi kutsatira malamulo. Iwo anali kunena kuti Paulo akuphunzitsa anthu kuti aiwale kusunga chilamulo, kuti anthu sayenera kudulidwa kapena kusunga miyambo ya makolo awo yoperekedwa ndi Mose. Izi sizinali zoona konse ayi, tsono atsogoleri a mpingo wa ku Yerusalemu anamulangiza kuti atenge akhristu anayi otsatira lamulo kuti apite nawo ku kachisi ndi kukadziyeretsa yekha kwa iwo.

Paulo anachita monga anamuuzira, koma pamene Ayuda anamuona m'kachisi, anayamba kunena kuti Paulo wabweretsa munthu wa mwa amitundu kulowa mkachisi. Sikoyenera kwa munthu wa mtundu wina kulowa mkachisi wa chiyuda mogwirizana ndi malamulo awo. Paulo sanachite zimenezi, koma kunali kotheka kufalitsa mbiri yabodzayi ndi kuwatsimikizira anthu kuti Paulo anaterodi. Choncho unyinji wonse wa Ayuda unankhamukira Paulo ndi kumgwira nati, "Amuna a Israyeli inu! Tithandizeni! Tithandizeni! Uyu ndiye munthu uja akunka naphunzitsa anthu zotsutsana ndi anthu a mtundu wathu kuti aliyense asatsatire chilamulo cha chiyuda. Akunenanso zoipitsa kachisi wa Mulungu ndi kumudetsa pobweretsa munthu amene sali Myuda mkati mwa kachisi."

Paulo anatulutsidwa kunja kwa kachisi ndipo zitseko za linga lozungulira kachisi zinatsekedwa kuti asatuluke.

Pamene anafuna kumupha, Mkulu woyang'anira asilikali a chiroma analandira uthenga wakuti ku Yerusalemu kwabuka chipolowe.

KUMANGIDWA KWA PAULO

Mkulu wa asilikaliyu analamula kuti Paulo amangidwe. Tsono anafunsa unyinji wa anthu amene anali pamenepo kuti Paulo ndani ndipo anachita chiyani.

Ena anali kungofuula zina enanso zina. Pamene mkulu wa asilikaliyu analephera kumva kalikonse chifukwa chongofuula wina zina ndi wina zina, analamula kuti Paulo apite naye ku linga la asilikali.

Pamene anafika pa masitepe olowera mkati mwa linga lija, asilikali anamunyamula pa mapewa kuopetsa anthu amene analalira moyo wake. Unyinji wa anthu unayamba kufuula kuti, "Mchotseni ameneyu apite basi!"

Asanamulowetse Paulo mkati mwa linga lija anapempha wolamulira asilikali uja kuti amulole kulankhula kwa anthu aja. Wolamulira uja anadabwa kumva Paulo akulankhula chigriki (chihelene). Kenaka Paulo anayamba kulankhula kwa anthu aja m'chihebri. (Werengani Machitidwe 22:1-21). Tsono pa pa nthawi imene Paulo anangotchula liwu lakuti, "amitundu" sanapitirire kulankhula chifukwa anthu anapfuula nanena kuti aphedwe msangamsanga! Tsono anali kukonzekera kumupha pamene mkulu wa asilikali anawaletsa. Anamtengera mkati mwa linga nalamulira asilikali kuti amkwapule mpaka Paulo aulule kulakwa kumene anachita. Mkuluyu anali kufuna kudziwa chifukwa chimene anthu aja anakwiya mwa mtundu wotere.

Pamene anam'manga Paulo kukonzekera kuti amkwapule iye anati, "Kodi malamulo anu amalola kukwapula mzika ya chiroma musanaweruze nkomwe mlandu wake?" Pamene mkulu wa asilikaliyu anamva kuti Paulo anali mbadwa ya chiroma anamtengera ku bwalo la chiyuda.

PAULO PA BWALO LA AKULU A CHIYUDA (SANHEDRIN)

Kwa nthawi zambiri Paulo anali kuwatengera Akhristu pa bwalo limeneli kukawazenga mlandu. Tsopano iye amene anaima pa bwaloli kuti aweruzidwe. Iye ayenera kuti anaunguzaunguza kuyang'ana ngati angampeze bwenzi lake. Iye anauza bwalolo kuti, "Abale anga, ndakhala moyo wanga wonse pamaso pa Mulungu ndi mtima wopanda kanthu konse koutsutsa,

mpaka lero." Mkulu wa ansembe, Hananiya, analamulira amene anali pafupi ndi Paulo kuti am'menye khofu pa kamwa. Kunyoza kotere kunamkwiyitsa Paulo ndipo analankhula mokwiya kwa Hananiya. Kenaka anapepesa, popeza sanadziwe kuti Hananiya anali mkulu wansembe.

Pa nthawi imeneyi ndi pamene Paulo anazindikira kuti pa'gululo panali Afarisi ndi Asaduki. Iye anadziwa kuti awa anali adani. Paulo analankhula momveka nati, "Abale anga ine ndine Mfalisi mwana wa Mfalisi." Izi zinautsa phokoso pakuti pa magulu awiriwa. Choncho mkulu wa asilikali anamchotsa Paulo kuopa kuti angamkadzule. Kachiwirinso anapulumuka ku imfa.

Usiku umenewo, Ambuye anachezera Paulo amene analibe m'ndende. Ambuye anati, "Usadandaule, Paulo; monga wawauzira anthu a ku Yerusalemu za Ine, chomwechonso ukanenere za Ine ku Roma." Tsopano Paulo anadziwa m'mene angapitire ku Roma koma sanadziwe kuti kudzamtengera nthawi yaitali motani kapena kuti zidzachitika bwanji.

APULUMUTSIDWA KUCHOKA KU YERUSALEMU

Ayuda, atasokonezeka mutu ndi Paulo, tsopano anatsimikiza kwenikweni kuti amuphe. Iwo analumbira kuti sadzadya kapena kumwa kufikira Paulo atafa. Mphwake wa Paulo anamva za chiwembu cha Ayuda ndipo anapita nakamuuza mkulu wa asilikali uja za chiwembucho. Mkulu wa asilikali analamula kuti Paulo aperekezedwe ndi asilikali a nthungo okwana 200 (mazana awiri) ndi ena okwera pa akavalo okwana 70 mpaka ku Kaisareya. Kumeneku, Paulo anamtengera kwa Felike naikidwa m'nyumba ya chifumu ya Herodi. Aka kanali kanthawi kenanso kamene Paulo anapulumuka ku imfa. Iye anakhala m'ndende zaka ziwiri ku Kaisareya, apa nkuti kutatsala zaka zitatu kuti amasulidwe.

Ndi chifukwa chiyani Paulo anayenera kukhala m'ndende pa nthawi imene inali yofunika kwambiri pa utumiki wake? Sitingathe kuyankha pfunso limeneli mwatsatanetsatane. Kwa Paulo, kunali kobvuta kuti amvetsetse koma kwa ife masiku ano tizindikira bwino chifukwa chake. Paulo anafunika kuti apume kokwanira. Zitatha zaka makumi awiri akuyenda ndi kugwira ntchito molimbika anafika pakutha phumi. Iyi sinali nthawi yopuma kokha komanso nthawi yolingirira zinthu zoona za Yesu Khristu. Pambuyo pake, Paulo analemba kalata kwa Afilipi ponena za kumangidwa kwake. "Abale, ndifuna kuti mudziwe kuti zimene zandigwera, makamaka zathandiza kufalitsa Uthenga Wabwino. Motero asilikali onse olonda nyumba ya mfumu, ndiponso ena onse kuno, adziwa kuti ndili m'ndende chifukwa cha Khristu."

OOOOOoOOOOO

PHUNZIRO 9

MUTU WA PHUNZIRO: PAULO PAMASO PA FESTO

MAWU OWERENGA: Machitidwe 26:1-32

MAWU APA MTIMA: "Taonani tsopano ndiyo nyengo yabwino yolandiridwa, taonani, tsopano ndilo tsiku la chipulumutso." 2 Akorinto 6:2

Paulo anazengedwa mlandu koyamba pamaso pa Felike. Uyu anali woweruza wa nkhaza ndi wopanda chilungamo. Amene anali kutsutsana ndi Paulo sanali Ayuda a ku Asia ayi koma a ku Yerusalemu. Iwo analipira ndalama kwa solisitala wodziwa malamulo kuti akawaimire pa mlandu womtsutsa Paulo ndipo dzina lake anali Tertulo. Tertulo anayamba kulankhula moyamikira Festo wa nkhazayo. Kenaka anapereka milandu iwiri ya Paulo:

1. Paulo anali munthu wa mpatuko wotchedwa "Anazarene."
2. Anadetsa kachisi wa Mulungu.

Paulo analibe solisitala koma ndi luso lakudziwa kulankhula anadziteteza mokwanira. Iye anawatsimikizira kuti sanadetse kachisi. Iye anawauza kuti anali mkhristu ndiponso kuti chikhristu ndicho chipembedzo chenicheni cha Ayuda. Paulo unamkomera mlandu kotero anayenera kumasulidwa. Koma Felike pochita mantha ndi atsogoleri achiyuda, sanagamule mlandu ndipo anangomusiya Paulo m'ndende.

PAMASO PA FESTO

Felike anali woweruza woipa kwambiri kotero kuti mfumu ya dzikolo, Nero anamchotsa pampando. M'malo mwake analowa ndi Porkiyo Festo. Uyu anali wabwino kwambiri kuposa Felike. Tsono chifukwa chakuti Festo anali woweruza watsopano, Ayuda anabwera kudzanena mlandu wa Paulo kachiwiri. Festo anapita ku Yerusalemu ku msonkhano wa Ayuda ndipo iwo anapempha kuti Paulo abwere naye ku Yerusalemu kuti adzazenge mlandu wake. Iwo anali kukonzekerabe kumupha Paulo. Festo anakana pempho lawo nawauza kuti apitirire kumuzengera ku Kaisareya komweko. Choncho Paulo anazengedwa mlandu kachiwiri tsopano pamaso pa Festo.

Ayuda anamunenera kuti anali kuyambitsa mabvuto pakati pa Ayuda, anali kupembedza Mulungu mwa chinyengo, ndi kuti anali kufuna kuukira boma. Festo anali munthu wosazindikira zambiri zokhudza miyambo ya chiyuda choncho iye anaganiza zomutenga Paulo ku bwalo la Sanhedrin (bwalo lalikulu la chiyuda) ku Yerusalemu. Paulo anadziwa kuti ku bwalo limeneli sakakhala ndi mwawi uliwonse. Tsono pakuti iye anali mzika

ya Chiroma, anali ndi mwawi wakutha kukana kupita ku Yerusalemu ndi kukazengedwa ku khothi la mfumu yaikulu m'dzikomo. Choncho Paulo anauza bwalolo kuti, "Nditulukira kwa Kaisara." Izi zinamdabwitsa Festo koma sakananenera mwina. Iye, mogwirizana ndi lamulo anayenera kungobvomera. Iye anati, "Wanena, 'Nditulukira kwa Kaisara' kwa Kaisara udzapita."

## PAMASO PA AGRIPA

Kusintha kunenaku kunampanga Festo kuti akhale wobvutika mumtima. Analibe chomtsutsa Paulo. Tsono kutumiza mlandu kwa mfumu yaikulu wopanda umboni wodziwika bwino, kukanampanga kukhala wopusa pamaso pa mfumu. Mwina akanachotsedwanso pampando wake. Mfumu Herode Agripa ndi mlongo wake anabwera kudzachezera Festo pa nthawiyi. Kunali koyenera kwa Festo kuwasangalatsa alendo ake monga m'mene akanathera. Tsono Festo anaona kuti alendo akhoza kusangalala atamva mlandu wa mkaidi amene anali kumusungayo. Agripa anali munthu wodziwa bwino za malamulo ndi miyambo ya chiyuda. Festo anaganiza kuti Agripa akhoza kumuthandiza kukonza mlandu wokautula kwa mfumu yaikulu ya chiroma. Nthawi inakonzedwa ndipo Paulo anabweretsedwa pa bwalo la milandu Agripa ndi amene anakhala mtsogoleri pa mlanduwu. Paulo anayamba kulankhula. Iye anafotokoza mwatsatanetsatane kuyambira nthawi imene anakumana ndi Yesu pa njira yonka ku Damasiko kufikira nthawi imene anagwidwa ndi kuikidwa m'ndende. Atatha apo, anayamba kulalikira Dzina la Yesu kwa bwanamkubwa Agripa poyembekezera kuti alandire Yesu monga Mpulumutsi wake. Festo, Agripa ndi ena anakhudzidwa kwambiri ndi Uthenga wa Paulo. Agripa atakhudzidwa ndi Uthenga anati kwa Paulo, "Kodi ukufuna kundikhalitsa mkhristu pa kanthawi komweka." Atsogoleri onse anabvomereza kuti Paulo sanachite kanthu koyenera imfa. Komabe iye sanamasulidwe.

## ULENDO WA PANYANJA WA KU ROMA

Patapita masiku pang'ono mlandu wake utamveka pamaso pa Agripa, Festo anakonza ulendo wa Paulo wonka ku Roma. Paulo ndi akaidi ena anasungidwa m'manja mwa mkulu woyang'anira asilikali dzina lake Yuliyo. Luka ndi Aristarko anapita naye Paulo. Iwo anayamba ulendo wawo molunjika ku gombe la ku Asia. Patatha tsiku limodzi anafika ku Sidoni ndipo Paulo analoledwa kuolokera kumtunda kukachezera abwenzi mumzinda. Kenaka anapalasira kumpoto kwa dziko la Cyprus mpaka ku Mura, mzinda wa ku Lusiya. Apa anakwera ngalawa imene inali kupita ku Italy. Patapita masiku angapo anafika pa malo otchedwa, 'Pokocheza Pokoma' (Fair Havens). Apa panali pa chisumbu cha ku Krete. Nthawi ya mphepo ya mkuntho inafika. Choncho Paulo anawachenjeza amene anali kumusunga kuti asapitirire pa malopo mpaka nyengo

ya mphepo ya mkunthoyo itatha. Koma anthu ambiri, kuphatikiza ndi woyendetsa ngalawayo ndiponso mwini wa ngalawayo, anaganiza zopita mpaka ku Foinike asanaime kudikira nthawi ya mphepo.

## MABVUTO PAFUPI NDI CHILUMBA CHA PA MALTA

Atachoka Pokocheza Pokoma paja anakonzekera kukafika ku Foinike pasanathe maola angapo. Koma mphepo yaikulu inadza niwakankhira ku chilumba cha Kauda. Apa anaima ndi kukonza mwina mofunikira pa ngalawayo.

Sakanatha kukhala pamalo amenewa chifukwa mphepo ikanawakankhira ku mpoto kwa dziko lino la Afrika. Choncho anayamba kutsitsa katundu wawo ndi kumponyera kunja kwa ngalawa kuti isalemedwe kwambiri. Kwa masiku angapo kunakhala kuli mitambo ndipo dzuwa silinaoneke kotero kuti ngakhale amalinyero sanazindikire kumene anali. Potsiriza anataya chikhulupiriro chonse chakuti akhoza kupulumuka.

Nthawi imeneyi ndi pamene Paulo analankhula kwa iwo nati, "Amuna inu, mukadamvera ine, osachoka ku Krete, zonse izi sizinakachitika. Komabe zonse zikhala bwino. Tidzapulumuka. Usiku omwe uno ndinaona m'ngelo wa Mulungu, ndipo anandiuza kuti ndikaonekera pamaso pa Kaisara ndipo moyo wa munthu aliyense muno sudzatayika."

Kwa masabata awiri, ngalawa ija inali kungokankhidwa uku ndi uku. Tsono usiku wina, amalinyero anamva mkokomo wa madzi okocheza pa gombe. Iwo anaponya anangula anayi m'madzi kuopa kuti ngalawayo ingagunde miyala ndi kuonongeka kufupi ndi doko. Choncho anadikira mpaka m'mawa.

Ena sanafune kudikira koma anafuna kutenga mabwato awo ndi kuolokera ku gombe. Koma Paulo anati, "pokhapokha ngati tonse tikhala mom'muno mpaka kutacha, ambiri afa" Choncho amalinyero sanaloledwe kuchoka pa mabwato awo.

Paulo anawalonjeza onse aja kuti palibe munthu mmodzi amene adzataya moyo wake. Iye anatenga mkate nayamika Mulungu. Onse anadya ndi kuyamika.

Kutacha, anayesanso kuponya katundu wina kunja kwa ngalawayo kuti ikafike bwino; koma inatsakamira mum'chenga.

Maganizo a asilikali aja anali akuti angopha akaidi onse kuopa kuti ena angathawe. Koma woyang'anira sanabvomereze izi. Iye anati, "Nonse amene mungathe kusambira tiyeni musambire mpaka ku gombe. Ngati simungathe kusambira, pezani thabwa lililonse limene lingakuyandamitseni mpaka ku gombe."

Choncho onse anakocheza pa chilumba cha Melita (Malta). Kunali kuzizira kwambiri, ndipo amuna anasonkha moto. Pamene Paulo ananyamula mtolo wa nkhuni kuti aponye pamoto, njoka inamkwera padzanja. Munthu wina pakuona izi anati, "Taonani, munthuyu ayenera kukhala chigawengadi. Anapulumuka bwino-bwino pa nyanja koma tsopano alandira chilango chomuyenera."

Paulo anaikatamulira pa moto njokayo mosabvunduka konse. Anthu anangoyang'ana ndi kuzizwa. "Dzanja lake linayenera kutupa. Ayenera kuti afa basi!"

"Hi ndi mulungu amene" anatero monong'ona poona kuti Paulo sakugwa ndi kulumidwa ndi njoka.

Tsopano Popliyo amene anali munthu wodziwika ndi wofunika kwambiri pa chilumbacho, anaitanira alendowo kunyumba kwake. Paulo anakapeza kuti bambo wake wa munthuyu anali kudwala malungo ndi kamwazi. Pamene Paulo anampemphe-rera bamboyo, Mulungu anamchiritsa. Posachedwa ena anabwera ndi odwala awo kuti adzachiritsidwe.

Patapita miyezi itatu Paulo ndi ena ananyamuka ulendo wonka ku Roma. Anthu a pa chilumba chija anawapatsa iwo mphatso zambiri ndi mitulo. Uthenga unafika ku Roma wakuti Paulo alikubwera.

00000o00000

PHUNZIRO 10

MUTU WA PHUNZIRO: PAULO KU ROMA

MAWU OWERENGA: Machitidwe 28:16-31

MAWU APA MTIMA: "Pakuti kwa ine kukhala ndi moyo ndiko Khristu ndi kufa kuli kupindula." Afilipi-1:21

Ngalawa imene anakwera Paulo inakocheza ku doko la ku Napo, mtunda wosachepera 220 kilometres kuchokera ku Roma. Paulo anakondwa kwambiri pamene magulu awiri a akhristu a ku Roma anakumana naye panjira pa mtunda wa 70 kilometres kuchokera ku Roma. Iwo anayenda pansi kuchokera pamenepo kukafika ku Roma.

Potsiriza pake, Paulo anafika ku mzinda umenewu umene unali likulu la dziko lonse limene linali pa ulamuliro wa chiroma. Uwu unali mzinda wofunika kwambiri kuposa yonse pa nthawiyo.

KUIKIDWA M'NDENDE KWA PAULO

Pamene anafika ku Roma, akaidi onse anaikidwa m'ndende kupatula Paulo. Pa zifukwa zina Paulo anali kulandira ulemu wa padera kuposa ena onse. Paulo anamangidwa unyolo pamodzi ndi amene anali kumulonda, mdindo wa ndende, koma anali kumulola kukakhala kunyumba kutali ndi nyumba ya ndende. Anali kuloledwa kuchezeredwa ndi alendo nthawi zonse.

Analipo Ayuda ambiri amene anali kukhala mumzinda wa ku Roma. Patatha masiku atatu chifikire ku Roma, Paulo anaitanitsa akuluakulu a chiyuda pamodzi. Iye anawafotokozera zonse zimene zinamuonekera kuti apezeke wa msinga. Iwo anamuuza kuti sanalandire kalata iliyonse kuchokera ku Yerusalemu. Iwo anaonetsa chidwi chofuna kudziwa kuti chikhristu ndi chiyani. Tsono onsewo anapanga tsiku lakuti adzamve okha ulaliki wa Paulo. Pa tsiku limeneli anthu ambiri anadza kudzamvera ulaliki wa Paulo za Uthenga Wabwino wa Yesu Khristu. Kuyambira m'mawa mpaka madzulo Paulo anafotokoza bwino zoona za chikhristu. Ena anakhulupirira koma ena anaukana. Paulo anawauza kuti adzakhala akuphunzitsa anthu amitundu nthawi zambiri.

Paulo anali kuyembekezera kuti mlandu wake uzengedwa posachedwa ndi kumasulidwa. Zaka ziwiri zinapita akuyembekezerabe mlandu. Iye anapitirira kulalikira ndi kuphunzitsa ndipo analandira aliyense amene anabwera kudzamuona. Mumzaka zimenezi, anthu ambiri anamdziwa Yesu ndi kumulandira monga Mpulumutsi wawo.

MAKALATA OLEMBEDWA NDI PAULO ALI KU NDENDE

Zaka ziwiri zimenezi ali ku Roma, Paulo anali wotanganidwa kwambiri. Iye sanangobweretsa anthu kwa Yesu kokha, komanso anapeza mpata wolemba makalata anayi, amene tsopano ali mabuku opezeka m'Chipangano Chatsopano. Awa ndi:

(I) AFILIPI
(II) AEFESO
(III) AKOLOSE
(IV) FILIMONE

AFILIPI

Kalata imeneyi analembera ku mpingo wa ku Filipi. Mpingowu unali umodzi wa mipingo imene Paulo anali kuikonda kwambiri. Mpingo umenewu utamva za bvuto la Paulo, unamtumizira chithandizo chokwanira. Kalata ya ku Afilipi inali ya chikondi ndi chiyamiko. Ngakhale kuti kalata imeneyi inachokera kwa Paulo ali ku ndende koma inali yodzala ndi chimwemwe, chilimbikitso, chikhulupiriro ndi chiyembekezo chosatha.

Tsono kupyolera mu zimene zinamchitikira Paulo tiyenera kuphunzira ndi kudziwa kuti ngati tidzipereka kwathunthu kwa Mulungu adzatithandiza kugonjetsa mabvuto athu.

Abwenzi mwa Ambuye ochokera ku madera akutalikutali anadza kudzamthandiza Paulo. Luka anali naye pamodzi ndipo Timoteo anali kubwera nthawi zambiri kudzamuona. Epafrodito anadza ndi mafuno abwino kuchokera ku mpingo wa ku Filipi ndipo iye anadzakhala ndi Paulo.

Koma tsiku lina Epafrodito anadwala kwambiri pafupi imfa. Paulo anamtuniza kwawo ndipo anampatsira kalata. Kalata imeneyi ndiyo ya kwa Afilipi.

Kalata imeneyi ya kwa Afilipi imapitirira ndi mawu otere:

"Chifukwa chake mumlandire mwa Ambuye, ndi chimwemwe chonse; nimuchitire ulemu oterewa; pakuti chifukwa cha ntchito ya Khristu anafikira pafupi imfa, wosasamalira moyo wake, kuti akakwaniritse chiperewero cha utumiki wanu kwa ine."

"Koma ndinakondwera mwa Ambuye kwakukulu, kuti tsopano munatsitsimukako kulingirira mtima za kwa ine, kumenekonso munalingiriraki, koma munasowa pochitapo. Sikuti ndinena monga mwa chiperewero, pakuti ndaphunzira ine, kuti zindikwanire zili zonse ndili nazo. Ndadziwa ngakhale kupeputsi-

dwa, ndadziwanso kusefukira; konseko ndi m'zinthu zonse ndalowa mwambo wa kukhuta, ndiponso wakumva njala; wakusefukira ndiponso wakusowa. Ndikhoza zonse mwa Iye wondipatsa mphamvu."

Koma ndili nazo zonse, ndipo ndisefukira; ndadzazidwa, popeza ndalandira kwa Epafrodito zija zidachokera kwanu, koma Mulungu wanga adzakwaniritsa chosowa chanu mu ulemerero mwa Khristu Yesu. Tsono inu khalani a chimwemwe pakuti ndinu ake. Phunzirani kusadandaula, koma mupempheni m'mapemphero anu chilichonse icho muchisowa, ndi kumuyamika pamene muli kupemphera. Ndipo mudzakhala ndi chitonthozo cha Mulungu chopitirira maganizo athu."

"Kumbukirani, choonadi chonse, ndi chilichonse chimene chili chokhulupirika ndi cha chilungamo ndi changwiro ndi chokondeka, ikani maganizo anu pa zinthu zimenezi. Pitirizani kuchita monga ndakuphunzitsirani, ndi kuchita zimene mwandiona ine ndikuchita."

"Sikunena kuti ndinalandira kale, kapena kuti ndatha kukonzeka wamphumphu; koma ndilondetsa, ngatinso ndikachigwire ichi chimene anandigwirira Yesu Khristu. Abale, ine sindiwerengera ndekha kuti ndatha kuchigwira; koma chinthu chimodzi ndichichita; poiwaladi zam'mbuyo ndilondetsa polekezerapo, kutsatira mfupo wa maitanidwe akumwamba a Mulungu a mwa Yesu."

"Abale kuno akulonjerani."

## FILEMONI

Kalata ya kwa Filemoni ndi yosiyana ndi makalata ena onse a Paulo. Iyi ndi mbiri imene Paulo anali kuyanjanitsa abale awiri amene iye anawabweretsa kwa Yesu. Pamene Paulo anali ku Efeso anakumana ndi anthu a ku Asia. M'modzi mwa iwo anali munthu wa chuma ndi wotchuka wa ku Kolose. Munthu ameneyu anali Filemoni ndipo analandira Yesu Khristu atamva kulalikira kwa Paulo. Filemoni anakhala mtsogoleri wa akhristu kudera la kwawo. Anthu amadzakumana m'nyumba mwake popembedza.

Filemoni anali ndi kapolo mmodzi, ngati panalibenso ena ambiri. Dzina la kapolo ameneyu anali Onesimo amene anafunafuna kukhala mfulu naganiza zothawira mbuye wake. Iye anathawadi ndipo zikukhala ngati kuti anabanso ndalama za mbuye wake Filemoni. Iye anauyatsa ulendo wopita ku Roma. Tsono anamva Paulo akulalikira. Paulo anambweretsa kwa Yesu namlandira monga Mpulumutsi wake ndipo anamulangiza kuti abwerere kwa mbuye wake Filemoni ku Kolose. Poyamba Filemoni anakayika. Iye sanafune kukapitirira kukhala kapolo chifukwa

tsopano anali womasuka. Paulo anamuuzitsa kuti ayenera kubwerera chifukwa pa kutero aonetsa chikhristu chake. Paulo anamulonjeza kuti alemba kalata kwa Filemoni kumfotokozera zonse zinachitika. Potsiriza, Onesimo anabvomera kubwerera ndipo Paulo anampatsira kalata imeneyi. Paulo anapempha Filemoni kuti Onesimo asakhalenso kapolo koma mfulu. Ngakhale anatero anati, "sikukulamulira kapena kukakamiza koma ufulu wa iwe mwini."

Tikhoza kumuyamikira Paulo chifukwa iye anali wofunitsitsa kubwerera ku mipingo imene anaiyamba posachedwa koma sanathe kutero. Komanso, chifukwa cha ichi, sanagwe mphwayi koma anapeza njira yokhayo imene akanatha kulimbikitsira nayo mipingo ndiyo kupyolera m'makalata.

00000o00000

PHUNZIRO 11

MUTU WA PHUNZIRO: PAULO M'NDENDE

MAWU OWERENGA: Aefeso 2:1-10

MAWU APA MTIMA: "Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo cha kuchita mwa chikhulupiriro, ndipo ichi chosachokera kwa inu: Chili mphatso ya Mulungu." Aefeso 2:8.

M'phunziro lapitali taphunzira kuti ngakhale Paulo anali m'ndende, anabweretsabe anthu ambiri kwa Yesu. Koma analembanso makalata ku mipingo imene anaiyamba; makalata amene tikuwawerengabe ngakhale masiku ano potilangiza bwino m'mipingo mwathu. M'phunziro lino tiphunzira za makalata awiri otsiriza a Paulo amene analemba ali kundendenso.

KALATA YA KWA AKOLOSE

Mpingo wa kwa Akolose unayambika pa nthawi imene Paulo anakhala zaka zitatu mumzinda wa ku Efeso. Sitidziwa ngati Paulo anayamba wachezera mpingo umenewu, koma anawadziwa bwino atsogoleri ake ndipo anakondweretsedwa nawo. Iye pamene anali m'ndende anamva za ziphunzitso zonyenga zimene zinafalikira m'dera limenelo la dziko la Asia. Zinali kuoneka kuti mpingo wa ku Efeso ndi wa ku Kolose ndiyo mipingo imene inakhudzidwa ndi ziphunzitso zimenezo. Choncho Paulo anadera nkhawa ndi mipingoyo ndipo analemba izi: "Pakuti ndingakhale ndili kwina, komatu mumzimu ndili pamodzi ndi inu, ndiyamika Mulungu kuti ndinu ake a Ambuye Yesu Khristu amene anadza kudzatisonyeza m'mene Mulungu alili."

"Tsono pakuti mumdziwa Yesu, mukhale monga Iye. Mwataya njira zanu za kupsya mtima ndi kunena bodza kwanu. Khalani ofatsa, a chikondi ndi okhululukira ena. Chilichonse chimene muchita, chitani mwa Ambuye ndi mtima wanu wonse."

"Musalole kuti wina akuphunzitseni zokhulupirira milungu ina. Khristu yekha adzakupatsani zosowa zanu, pakuti Mulungu anampatsa Iye mphamvu ndi ulemerero."

AEFESO

Kalata ya kwa Aefeso mwina inali ya kwa onse, kutanthauza kuti ikanatha kuwerengedwa ndi mpingo wina kenaka ndi kuitumizanso kwina m'dera lomwelo. M'kalata imeneyi muli mawu otere:

"Inu amitundu munakhala mukumva kuti simungathe kukhala m'banja la Mulungu. Tsopano inu muli kudziwa kuti izi si-

zoona konse. Pakuti Khristu anagumula khoma limene linatile kanitsa, chifukwa chakuti timkonda Iye, tonse (Ayuda ndi amitundu) tikhulupirira mwa Atate. Inde, tsopano sindinu akutali kapena alendo. Tonse ndife ziwalo za m'banja la Mulungu. Tonse pamodzi tilikumanga kachisi wake. Aneneri ndi atumwi aja ndiwo maziko, Yesu Khristu ndi mwala wa pangodya, tsono ife ndife nyumba."

"Musadandaule chifukwa chakukhala kwanga m'nsinga. Pakuti ngakhale ndili wamng'ono kwambiri pakati pa iwo okonda Mulungu, anandipatsa mphatso yakutha kukulalikirani Uthenga Wabwino ndi zozizwitsa za chikondi cha Mulungu kwa ife. Ndili kukupemphererani kuti Yesu adzakhala m'mitima mwanu mwachikhulupiriro ndi kuti mudzazindikire nokha chikondi chake. Nchachikuludi chikondi cha Yesu ndipo chipitirira zimene tingathe kuganizira."

"Ndine pano, wa m'ndende, kukupemphani kuti muchite monga akhristu. Khalani a bata ndi ofatsa. Sindinunso ofanana ndi m'mene munalili musanakhale akhristu. Tayani za kupsya mtima, zolongolola. Khalani a chifundo wina ndi mnzake, ofatsa okhululukirana wina ndi mnzake, monga Mulungu anakukhululukirani kaamba ka Yesu."

Pamene Paulo anali kulemba kalatayi, anali kuyang'ana msilikali amene anali kumlindirira. Chikopa (chisyango) ndi lupanga, cha pachifuwa, chobvala m'miyendo, nsapato ndi lamba - Izi ndi zomwe zinapanga yunifolomu ya msilikali wa chiroma. Iye anapitirira kulemba kalata yake kwa Aefeso:

"Mudzakhala mukumenyana ndi adani amene simungathe kuwaona, osati asilikali a anthu koma adani oipa m'chikhalidwe chonse. Bvalani zida zonse za Mulungu podziteteza nokha kwa choipa. Imani ndi kumenyana nawo adani a Mulungu."

Dzukani! lamba wanu ndi choonadi, cha pachifuwa chanu ndi chilungamo. M'mapazi anu bvalani nsapato za Uthenga Wabwino wa mtendere wa Mulungu. Tengani chisyango chanu cha chikhulupiriro kuti mudziteteze ku mibvi yoyaka ya woipayo. Chisoti chanu ndicho mawu a Mulungu."

Konzekerani nkhondo. Pamene mwachita zonse monga mwa kukwanitsa kwanu, pitiriranibe kumenya nkhondo."

"Pempherani ndi kupitirira kupemphera. Pemphererani onse okonda Yesu, makamaka inenso, kuti ndipitirire kulankhula mopanda mantha, ndingakhale kuti ndli wa m'nsinga."

"Mtendere kwa inu ndi chikondi.
Paulo mtumwi wa Khristu wodzozedwa ndi Mulungu."

Patatha zaka ziwiri, Paulo anamasulidwa ku ndende. Tilibe mbiri yolembedwa m'Buku Lopatulika yonena za izi koma mabuku akale a ku madera amenewa amafotokoza kuti Paulo anapitirira kuchezeranso mipingo ku Greece, Makedoniya, ndi mzigawo za ku Asia Minor.

00000o00000

PHUNZIRO 12

MUTU WA PHUNZIRO: MASIKU OTSIRIZA A PAULO

MAWU OWERENGA: 2 Timoteo 2:1-15

MAWU APA MTIMA: "Uchite changu kudzionetsera kwa Mulungu wobvomerezeka, wa ntchito wopanda chifukwa cha kuchita manyazi, wolunjika nawo mawu a choonadi." 2 Timoteo 2:15

Pamene Paulo anamasulidwa ku ndende anapitanso ku mipingo imene anaiyamba kale. Paulo ayenera kuti anali ndi chidwi chachikulu pa mipingo imeneyi ndipo anafunitsitsa kupitako mwamsanga.

## KU KRETE

Pa chilumba cha pa Krete panali anthu zikwizikwi. Kumamveka kuti pa chilumbacho panali mizinda yokwana zana limodzi. Anthu ake anali oipa ndi osalabadira za Mulungu. Amuna ndi akazi anali zidakwa zokhazokha. Anali zigawenga zimene zinali kuba m'ngalawa zodutsa pa chilumbachi. Komanso pa chilumbachi panali Ayuda amene anali kuchita malonda ndipo anali otchuka pa ntchito yawo. Tito anatumizidwa pa chilumbachi monga mtumwi. Zikukhala ngati kuti Paulo anakhala ndi Tito kwa kanthawi kena. Ntchito ya ku Krete inali yopambana ndithu. Ambiri analandira Yesu kukhala Mpulumutsi wawo.

Kenaka Paulo analemba kalata kwa Tito kumuuza m'mene angagwirire ntchito ndi mipingo ya ku Krete. Mkalata imeneyi, Paulo anapempha Tito kuti akakomane naye ku Nikapoli. Tito mwina mwake anali ndi Paulo pamene anaikidwa m'ndende kachiwiri.

## KUPSYA KWA MZINDA WA KU ROMA

Dziko la Aroma linakhala likulamulidwa ndi anthu a nkhaza, koma Nero anali woipa kuposa onse. Iye analamulira ufumu wa Chiroma kwa zaka 14. Nero anachita dumbo la mtundu wina uliwonse. Iye anapha amayi ake enieni omubereka. Anaphanso akazi ake angapo ndiponso abwenzi. Mbiri yakale imatiuza kuti Nero ndi amene anayatsa mzinda wa Roma. Nero anadziyesa yekha kukhala wodziwa kuimba kwambiri. Iye anaganiza kuti akayatsa mzinda wa Roma, akanakhoza kuimba mosangalala akuyang'ana ku malawi a motowo. Iye amakonda kuimba mkangala. Mzindawu unakhala ukupsya kwa masiku asanu ndi limodzi. Anthu a ku Roma anayamba kuwawidwa moyo ndipo anakwiya kwambiri chifukwa cha kupsya kwa mzindawo. Choncho, Nero anati kuti Akhristu ndi amene anaotcha mzindawo.

Chifukwa cha ichi Akhristu zikwizkwi anatenthedwa ndi moto mpaka imfa.

Pa nthawiyo, Paulo mdi amene anadziwika kuti ndiye mtsogoleri wa Akhristu, choncho moyo wake unali pa tsoka lalikulu.

## KUGWIDWA KWA PAULO

Pamene Paulo anamangidwa kachiwiri, ayenera kuti anaikidwa m'ndende m'mene munali mozizira kwambiri, komanso moopsya ndi mwa mdima wosaneneka. Pa nthawi imeneyi, Paulo sanachezeredwe ndi abwenzi ake kuopa kuti angadzaphedwe.

Paulo nkuti atalemba kalata imodzi kwa Timoteo pamene anali kuchezera mipingo kwa nthawi yotsiriza.

Timoteo anakhala mkhristu pamene Paulo anakachezera mzinda wa Lustra kwa nthawi yoyamba. Bambo wake anali wochokera mwa amitundu ndipo mayi wake Myuda wodzipereka. Analidi mnyamata wabwino kotero kuti Paulo anamtenga pa ulendo wake wachiwiri. Kuyambira pa nthawi imeneyi, Timoteo anali mtsogoleri wa mphamvu mumpingo. Paulo anamutcha Timoteo monga "mwana wake weniweni m'chikhulupiriro." Pambuyo pake, Timoteo anakhala mbusa wa ku mpingo wa ku Efeso.

## MAKALATA A PAULO KWA TIMOTEO

Pamene Paulo anali m'ndende kachiwiri, analemba kalata ina kwa Timoteo. M'makalata a kwa Timoteo mukupezeka mawu otere:

"Mwana wanga wokondeka,
"Khala msilikali wa mphamvu mwa Yesu Khristu ngakhale zinthu zibvute. Kumbukira nthawi zonse chimene unachikhulupirira. Kumbukira anthu amene anasunga chikhulupiriro chawo ndi kukusiyira. Pitirira kumenya nkhondo yabwino. Gwiritsa chimene uli nacho."

Pitirira kugwira ntchito kuti Mulungu akubvomereze, werenga mawu a Mulungu, ndipo udzakhala wa ntchito amene sudzachita manyazi.

Timoteo, ndikuyamika Mulungu m'mapemphero anga usiku ndi usana chifukwa cha iwe. Ndikufunitsitsa ndikanakuona. Kumbukira mphatso yako ya kuphunzitsa mumphamvu ya Mzimu wa Mulungu ndi chikondi.

"Mpang'ono pomwe usachite nane manyazi chifukwa cha kukhala kwanga m'ndende. Ine sindikuchita manyazi. Pakuti ndikudziwa kuti adzandisunga ndi chikhulupiriro chimene

ndinamkhulupirira nacho mpaka muyaya."

"Timoteo, tayesa kubwera kudzandiona msanga, isanafike nyengo yachisanu, unditengere chobvala chija ndinachisiya ku Trowa. Ndiponso mabuku, ubweretse mabuku. Ubwere posachedwa. Luka ndi yekhayo amene ali nane kuno tsopano. Dema anandisiya ndipo ndinamtuma Tukiko ku Efeso. Ubwere ndipo umtenge Marko. Uyesetse kubwera msanga."

"Ine sindikuchita mantha. Ndikudziwa kuti sindikhala ndi moyo nthawi yaitali, ndipo ndakonzeka kupita. Ndalimbana nako kulimbana kwabwino. Ndatsiriza ntchito yanga. Ndasunga chikhulupiriro. Ambuye, amene ali woweruza wolungama, wandisungira mphotho, ndi kwa tonsefe amene timkonda Iye.... koma, Timoteo, chonde fulumira."

Sitidziwa ngati Timoteo anakafikadi kwa Paulo iye asanaphedwe. Mawu amenewa ndiwo otsiriza a Paulo.

Komanso mawu awa amatsiriza bwino pa mbiri ndi moyo wa mtumwi Paulo — Wotsatira Yesu woposa onse, mtumwi wa mphamvu kuposa onse ndi mphunzitsi wamkulu wa Uthenga Wabwino kuposa onse.

oooooooooo0oooooooooo